yandikira ku mudzi umene analikupi-
tako; ndipo [a] anacita ngati anafuna
kupitirira. 29 Ndipo anamuumiriza
Iye, nati, Khalani ndi ife; pakuti
kuli madzulo, ndipo dzuwa lapende-
katu. Ndipo analowa kukhala nao.
30 Ndipo kunali m'mene Iye anaseama
nao pacakudya, [c] anatenga mkate,
naudalitsa, naunyema, napatsa iwo.
31 Ndipo maso ao anatseguka, ndipo
anamzindikira Iye; ndipo anawaka-
nganukira Iye, nawacokera. 32 Ndipo
anati wina kwa mnzace, Mtima wathu
sunali wotentha m'kati mwathu nanga
m'mene analankhula nafe m'nji-
ra, m'mene anatitsegulira malembo?
33 Ndipo ananyamuka nthawi yomwe-
yo nabwera ku Yerusalemu, napeza
khumi ndi mmodziwo, ndi iwo anali
nao atasonkhana pamodzi, 34 nanena,
Ambuye anauka ndithu, [i] naonekera
kwa Simoni. 35 Ndipo iwo ana-
wafotokozera za m'njira, ndi umo
anadziwika nao m'kunyema kwa
mkate.

*Yesu aonekera kwa khumi ndi mmodziwo.*

(Yoh. 20. 19-23.)

36 Ndipo pakulankhula izi iwowa,
[n] Iye anaimirira pakati pao; nanena
nao, Mtendere ukhale nanu. 37 Ko-
ma anaopsedwa ndi kucita mantha,
[o] nayesa alikuona mzimu. 38 Ndipo
anati kwa iwo, Mukhala bwanji obvu-
tika? ndipo matsutsano amauka
bwanji m'mtima mwanu? 39 Pe-
nyani manja anga ndi mapazi anga,
kuti Ine ndine mwini: [s] ndikhudzeni,
ndipo penyani; pakuti mzimu ulibe
mnofu ndi mafupa, monga muona

[a] Marko 6. 48
[b] Yoh. 21. 5
[c] Mat. 14. 19
[d] Mac. 10. 41
[e] Mat. 16. 21
[f] v. 32
[g] Mat. 16. 21
[h] Deut. 18. 15
Sal. 22.
Yes. 53.
[i] 1 Akor. 15. 5
[j] Mac. 13. 38
[k] Mat. 28. 19
[l] Mac. 1. 8
„ 5. 31, 32
[m] Yow. 2. 28
Mac. 2. 1-
[n] Marko 16. 14
[o] Marko 6. 49
[p] Marko 16. 19
[r] Mat. 28. 9, 17
[s] Yoh. 20. 20, 27
[t] Mac. 2. 46
„ 5. 42

ndiri nazo Ine. 40 Ndipo m'mene
ananena ici, anawaonetsera iwo manja
ace ndi mapazi ace. 41 Koma pokhala
iwo cikhalire osakhulupirira cifukwa
ca cimwemwe, nalikuzizwa, anati kwa
iwo, [b] Muli nako kanthu kakudya
kuno? 42 Ndipo anampatsa Iye ci-
dutsu ca nsomba yokazinga. 43 Ndipo
[d] anacitenga, nacidya pamaso pao.
44 Ndipo anati kwa iwo, [e] Awa ndi
mauwo ndinalankhula nanu, paja
ndinakhala ndi inu, kuti ziyenera
kukwanitsidwa zonse zolembedwa za
Ine m'cilamulo ca [f] Mose, ndi aneneri,
ndi masalmo. 45 Ndipo [g] anawatse-
gulira mitima yao, kuti adziwitse ma-
lembo; 46 ndipo anati kwa iwo,
[h] Kotero kwalembedwa, kuti Kristu
amve zowawa, nauke kwa akufa
tsiku lacitatu; 47 ndi kuti kulalikidwe
m'dzina lace kulapa ndi [j] kukhululu-
kidwa kwa macimo kwa [k] mitundu
yonse, kuyambira ku Yerusalemu.
48 [l] Inu ndinu mboni za izi. 49 Ndipo
onani, [m] Ine nditumiza pa inu lonje-
zano la Atate wanga; koma khalani
inu m'mudzi muno, kufikira mwa-
bvekedwa ndi mphamvu yocokera
Kumwamba.

*Yesu akwera kunka Kumwamba.*

(Mac. 1. 9-11.)

50 Ndipo anaturuka nao kufikira ku
Betaniya; nakweza manja ace, na-
wadalitsa. 51 Ndipo kunali, [p] pakuwa-
dalitsa Iye analekana nao, natenge-
dwa kunka Kumwamba. 52 Ndipo
[r] anamlambira Iye, nabwera ku Yeru-
salemu ndi cimwemwe cacikuru;
53 ndipo [t] anakhala cikhalire m'kacisi,
nalikuyamika Mulungu. Amen.

UTHENGA WABWINO WA

# YOHANE

1 *Umulungu wa Yesu Kristu.*

(Ahebr. 1. 5-13.)

[a] PACIYAMBI panali Mau, ndipo
Mau anali [b] kwa Mulungu, ndipo Mau
[c] ndiye Mulungu. 2 [d] Awa anali pa-
ciyambi kwa Mulungu. 3 [e] Zonse
zinalengedwa ndi Iye; ndipo kopanda
Iye sikunalengedwa kanthu kali konse
kolengedwa. 4 [g] Mwa Iye munali
moyo; ndi [i] moyowu unali kuunika
kwa anthu. 5 Ndipo [j] kuunikaku

[a] Akol. 1. 17
[b] Yoh. 17. 5
[c] Afil. 2. 6
[d] Gen. 1. 1
[e] Akol. 1. 16
[f] Malaki 3. 1
Mat. 3. 1
[g] Yoh. 5. 26
[h] Mac. 19. 4
[i] Yoh. 8. 12
[j] Yoh. 3. 19

kunawala mumdima; ndi mdimawu
sunakuzindikira.

*Utumiki wa Yohane Mbatizi.*

(v. 29-34. Mat. 3. 1-17. Marko 1. 1-11. Luka 3. 1-23.)

6 [f] Kunali munthu, wotumidwa ndi
Mulungu, dzina lace ndiye Yohane.
7 [h] Iyeyu anadza mwa umboni kudza-
cita umboni za kuunikaku, kuti onse
akakhulupirire mwa iye. 8 Iye si-





ndiye kuunikaku, koma anatumidwa
kukacita umboni wa kuunikaku.

*Yesu Kristu kuunika koona kutifikira mwa kubadwa m'thupi.*

9 [c] Uku ndiko kuunika kweni
kweni, kumene kuunikira anthu onse
akulowa m'dziko lapansi. 10 Anali
m'dziko lapansi, ndi dziko linalenge-
dwa ndi Iye, koma dziko [d] silinamzi-
ndikira Iye. 11 [f] Anadza kwa zace
za Iye yekha, ndipo ace a mwini
yekha sanamlandira Iye. 12 Koma
[i] onse amene anamlandira Iye, kwa
iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana
a Mulungu, kwa iwotu, akukhulu-
pirira dzina lace; 13 [j] amene sana-
badwa ndi mwazi, kapena ndi cifu-
niro ca thupi, kapena ndi cifuniro
ca munthu, koma ca Mulungu.
14 Ndipo [l] Mau anasandulika thupi,
nakhazikika pakati pa ife, ndipo
[n] tinaona ulemerero wace, ulemerero
wonga wa wobadwa yekha wa Atate,
wodzala ndi cisomo ndi coonadi.

*Umboni wa Yohane Mbatizi.*

(Mat. 3. 1-12. Marko 1. 1-8. Luka 3. 1-18.)

15 Yohane acita umboni za Iye,
napfuula nati, Uyu ndiye amene ndi-
nanena za Iye, [p] Wakudzayo pambuyo
panga analipo ndisanabadwe ine;
[r] cifukwa anakhala woyamba wa ine.
16 Cifukwa [s] mwa kudzala kwace
tinalandira ife tonse, cisomo cosinthana
ndi cisomo. 17 Cifukwa [t] cilamulo
cinapatsidwa mwa Mose; [v] cisomo
ndi coonadi zinadza mwa Yesu Kristu.
18 [w] Kulibe munthu anaona Mulungu
nthawi zonse; Mwana wobadwa
yekha wakukhala pa cifuwa ca Atate,
Iyeyu anafotokozera.
19 Ndipo umene ndiwo umboni wa
Yohane, pamene Ayuda anatuma kwa
iye ansembe ndi alembi a ku Yerusa-
lemu akamfunse iye, Ndiwe yani?
20 Ndipo [y] anabvomera, wosakana;
nalola kuti, Sindine Kristu. 21 Ndipo
anamfunsa iye, Nanga bwanji? ndiwe
Eliya kodi? Nanena iye, Sindine iye.
Ndiwe Mneneriyo kodi? Nayankha,
Iai. 22 Cifukwa cace anati kwa iye,
Ndiwe yani? kuti tibwezere mau kwa
iwo anatituma ife. Unena ciani za
iwe wekha? 23 Anati, [z] Ndine mau
a wopfuula m'cipululu, Lungamitsani
njira ya Mbuye, monga anati Yesaya
mneneriyo. 24 Ndipo otumidwawo
anali a kwa Afarisi. 25 Ndipo ana-
mfunsa iye, nati kwa iye, Koma
ubatiza bwanji, ngati suli Kristu,

[a] Mat. 3. 11
v. 15
[b] Mat. 3. 11
v. 15
[c] Yes. 49. 6
[d] Yoh. 16. 3
[e] Yes. 53. 7
v. 36
Mac. 8. 32
[f] Luka 19. 14
[g] Agal. 1. 4
[h] v. 15, 27
[i] Aroma 8. 15
[j] Yoh. 3. 5, 6
[k] Mat. 3. 6
[l] Luka 1. 31, 35
[m] Mat. 3. 16
[n] Mat. 17. 2
[o] Mat. 3. 11
Mac. 2. 1-
[p] Mat. 3. 11
[r] Yoh. 8. 58
[s] Aefeso 1. 6
[t] Deut. 4. 44, 45
[u] Yes. 53. 7
v. 36
Mac. 8. 32
[v] Yoh. 14. 6
[w] Eks. 33. 20
Mat. 11. 27
[y] Yoh. 3. 28
[z] Mat. 3. 3
[a] Mat. 16. 17, 18

kapena Eliya, kapena Mneneriyo?
26 Yohane anawayankha, nati, [a] Ine
ndibatiza ndi madzi; pakati pa inu
paimirira amene simumdziwa, 27 [b] ndi-
ye wakudza pambuyo panga, amene
sindiyenera kummasulira lamba la
nsapato yace. 28 Zinthu izi zinacitika
m'Betaniya tsidya lija la Yordano,
pomwe analikubatiza Yohane.
29 M'mawa mwace anaona Yesu
alinkudza kwa iye, nanena, [e] Onani
Mwanawankhosa wa Mulungu [g] amene
acotsa cimo lace la dziko lapansi!
30 [h] Ndiye amene ndinati za Iye,
Pambuyo panga palinkudza munthu
amene analipo ndisanabadwe ine;
pakuti anali woyamba wa ine. 31 Ndi-
po sindinamdziwa Iye; koma kuti
aonetsedwe kwa Israyeli, [k] cifukwa ca
ici ndinadza ine kudzabatiza ndi
madzi. 32 Ndipo Yohane anacita
umboni, nati, [m] Ndinaona Mzimu ali-
kutsika kucokera Kumwamba monga
nkhunda; nakhalabe pa Iye. 33 Ndi-
po sindinamdziwa Iye, koma wondi-
tumayo kudzabatiza ndi madzi, Iyeyu
ananena ndi ine, Amene udzaona
Mzimu atsikira, nakhala pa Iye, [o] ye-
mweyu ndiye wakubatiza ndi Mzimu
Woyera. 34 Ndipo ndaona ine, ndipo
ndacita umboni kuti Mwana wa
Mulungu ndi Yemweyu.

*Ophunzira oyamba a Yesu.*

35 M'mawa mwacenso analikuimi-
rira Yohane ndi awiri a akuphunzira
ace; 36 ndipo poyang'ana Yesu
alikuyenda, anati, [u] Onani Mwanawa-
nkhosa wa Mulungu! 37 Ndipo
akuphunzira awiriwo anamva iye ali-
nkulankhula, natsata Yesu. 38 Koma
Yesu anaceuka, napenya iwo aliku-
mtsata, nanena nao, Mufuna ciani?
Ndipo anati kwa Iye Rabi (ndiko
kunena posandulika, Mphunzitsi), mu-
khala kuti? 39 Nanena nao, Tiyeni,
mukaone. Pamenepo anadza naona
kumene anakhala; nakhala ndi Iye
tsiku lomwelo; panali monga ora
lakhumi. 40 Andreya mbale wace wa
Simoni Petro anali mmodzi wa awi-
riwo, anamva Yohane, namtsata Iye.
41 Anayamba iye kupeza mbale wace
yekha Simoni, nanena naye, Tapeza
ife Mesiya (ndiko kusandulika Kristu).
42 Anadza naye kwa Yesu. M'mene
anamyang'ana iye, anati, Uli Simoni
mwana wa Yohane; [a] udzachedwa
Kefa (ndiko kusandulika Petro).
43 M'mawa mwace anafuna kutu-
ruka kunka ku Galileya, napeza Filipo.
Ndipo Yesu ananena naye, Tsata ine.
44 Koma Filipo anali wa ku Betsaida,

mudzi wa Andreya ndi Petro. 45 Filipo anapeza Natanayeli, nanena naye, Iye [b] amene Mose analembera za Iye m'cilamulo, ndi aneneri, tampeza, ndiye Yesu mwana wa Yosefe wa ku Nazarete. 46 Natanayeli anati kwa iye, [c] Ku Nazarete nkutha kucokera kanthu kabwino kodi? Filipo ananena naye, Tiye ukaone. 47 Yesu anaona Natanayeli alinkudza kwa Iye, nanena za iye, Onani, M-israyeli ndithu, mwa iye mulibe cinyengo! 48 Natanayeli ananena naye, Munandidziwira kuti? Yesu anayankha nati kwa iye, Asanakuitane Filipo, pokhala iwe pansi pa mkuyu paja, ndinakuona iwe. 49 Natanayeli anayankha iye, Rabi, [f] Inu ndinu Mwana wa Mulungu, [g] ndinu Mfumu ya Israyeli. 50 Yesu anayankha nati kwa iye, Cifukwa ndinati kwa iwe kuti ndinakuona pansi pa mkuyu ukhulupirira kodi? udzaona zoposa izi. 51 Ndipo ananena naye, Indetu, indetu, ndinena ndi inu, [h] Mudzaona thambo lotseguka, ndi angelo a Mulungu akwera natsikira pa Mwana wa munthu.

## 2 *Yesu asandutsa madzi vinyo ku Kana.*

Ndipo tsiku lacitatu panali ukwati m'Kana wa m'Galileya; ndipo amace wa Yesu anali komweko. 2 Ndipo Yesu yemwe ndi akuphunzira ace anaitanidwa ku ukwatiwo. 3 Ndipo pakutha vinyo, amace wa Yesu ananena naye, Alibe vinyo. 4 Yesu nanena naye, [l] Mkazi, ndiri ndi ciani ndi inu? [n] nthawi yanga siinafike. 5 Amace ananena kwa atumiki, Cimene ciri conse akanena kwa inu, citani. 6 Ndipo panali pamenepo mitsuko yamiyala isanu ndi umodzi yoikidwako [o] monga mwa mayeretsedwe a Ayuda, yonse ya miyeso iwiri kapena itatu. 7 Yesu ananena nao, Dzazani mitsukoyo ndi madzi. Naidzaza, nde nde nde. 8 Ndipo ananena nao, Tungani tsopano, mupite nao kwa mkulu wa phwando. Ndipo anapita nao. 9 Koma pamene mkuluyo analawa madzi osanduka vinyowo, ndipo sanadziwa kumene anacokera (koma atumiki amene adatunga madzi anadziwa), mkuluyo anaitana mkwati, 10 nanena naye, Munthu ali yense amayamba kuika vinyo wokoma; ndipo anthu atamwatu, pamenepo wina wosakoma; koma iwe wasunga vinyo wokoma kufikira tsopano lino. 11 Ciyambi ici ca zizindikilo zace Yesu anacita m'Kana wa m'Galileya

[a] Yoh. 1. 14
[b] Deut. 18. 18
Yes. 9. 6
[c] Yoh. 7. 41, 42, 52
[d] Yoh. 11. 55
[e] Mat. 21. 12
Marko 11. 15
Luka 19. 45
[f] Mat. 14. 33
[g] Mat. 21. 5
[h] Luka 22. 43
Mac. 1. 10, 11
[i] Sal. 69. 9
[j] Mat. 12. 38
[k] Mat. 26. 61
Marko 14. 58
[l] Yoh. 19. 26
[m] Luka 24. 7, 8
[n] Yoh. 7. 6, 30
[o] Marko 7. 3
[p] Mat. 9. 4
Marko 2. 8
Mac. 1. 24
[r] Yoh. 7. 50
,, 19. 39
[s] Yoh. 9. 16, 33

[a] naonetsera ulemerero wace; ndipo akuphunzira ace anakhulupirira Iye. 12 Zitapita izi anatsikira ku Kapernao, Iye ndi amace, ndi abale ace, ndi ophunzira ace; nakhala komweko masiku owerengeka.

### *Yesu ayeretsa Kacisi poyamba paja.*

(Mat. 21. 12-17.)

13 Ndipo [d] Paskha wa Ayuda unayandikira, ndipo Yesu anakwera kunka ku Yerusalemu. 14 Ndipo [e] anapeza m'kacisi iwo akugulitsa ng'ombe ndi nkhosa ndi nkhunda, ndi akusinthana ndalama alikukhala pansi. 15 Ndipo pamene adapanga mkwapulo wazingwe, anaturutsa onse m'kacisimo, ndi nkhosa ndi ng'ombe; nakhuthula ndalama za osinthanawo, nagubuduza magome; 16 nati kwa iwo akugulitsa nkhunda, Cotsani izi muno; musamayesa nyumba ya Atate wanga nyumba ya malonda. 17 Akuphunzira ace anakumbukila kuti kunalembedwa, [i] Cangu ca pa nyumba yanu candidya ine. 18 Cifukwa cace Ayuda anayankha nati kwa iye, [j] Mutionetsera ife cizindikilo canji, pakuti mucita izi? 19 Yesu anayankha nati kwa iwo, [k] Pasulani kacisi uyu, ndipo masiku atatu ndidzamuutsa. 20 Pamenepo Ayuda anati, Zaka makumi anai ndi zisanu ndi cimodzi analimkumanga kacisiyu, kodi inu mudzamuutsa masiku atatu? 21 Koma Iye analikunena za kacisi wa thupi lace. 22 Cifukwa cace atauka kwa akufa, [m] akuphunzira ace anakumbukira kuti ananena ici; ndipo anakhulupirira colemba, ndi mau amene Yesu ananena.

23 Koma pamene anali m'Yerusalemu pa Paskha paphwando, ambiri anakhulupirira dzina lace, pakuona zizindikilo zace zimene anacitazi. 24 Koma Yesu sanakhulupirira iwo kuti akhale nao, cifukwa Iye anadziwa anthu onse, 25 ndipo sanasowa wina acite umboni za munthu; pakuti [p] anadziwa Iye yekha cimene cinali mwa munthu.

## 3 *Yesu aphunzitsa Nikodemo za kubadwa kwatsopano.*

Koma panali munthu wa Afarisi, dzina lace Nikodemo, mkulu wa Ayuda. 2 [r] Iyeyu anadza kwa Yesu usiku, nati kwa Iye, Rabi, tidziwa kuti Inu ndinu mphunzitsi wocokera kwa Mulungu; pakuti [s] palibe munthu akhoza kucita zizindikilo zimene





Inu mucita, ngati Mulungu sakhala naye. 3 Yesu anayankha nati kwa iye, Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, [a] Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu. 4 Nikodemo ananena kwa Iye, Munthu akhoza bwanji kubadwa atakalamba? Kodi akhoza kulowanso m'mimba ya amace ndi kubadwa? 5 Yesu anayankha, Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwa madzi ndi Mzimu, sakhoza kulowa ufumu wa Mulungu. 6 [c] Cobadwa m'thupi cikhala thupi, ndipo cobadwa mwa Mzimu, cikhala mzimu. 7 Usadabwe cifukwa ndinati kwa iwe, Uyenera kubadwa mwatsopano. 8 Mphepo iomba pomwe ifuna, ndipo ukumva mau ace, koma sudziwa kumene icokera, ndi kumene imuka; cotero ali yense wobadwa mwa Mzimu. 9 Nikodemo anayankha nati kwa Iye, [g] Izi zingatheke bwanji? 10 Yesu anayankha nati kwa iye, Kodi uli mphunzitsi wa Israyeli, ndipo sudziwa izi? 11 [i] Indetu, indetu, ndinena kwa iwe, Tilankhula cimene ticidziwa, ndipo ticita umboni za cimene taciona; ndipo umboni wathu simuulandira. 12 Ngati ndakuuzani za pansi pano, ndipo simukhulupira, mudzakhulupira bwanji, ngati ndikuuzani za Kumwamba? 13 Ndipo [l] kulibe munthu anakwera Kumwamba, koma Iye wotsikayo kucokera Kumwamba, ndiye Mwana wa munthu, wokhala m'Mwambayo. 14 Ndipo [n] monga Mose anakweza njoka m'cipululu, cotero Mwana wa munthu ayenera kukwezedwa; 15 kuti [p] yense wakukhulupira akhale nao moyo wosatha mwa Iye.

16 Pakuti [r] Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira Iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha. 17 Pakuti [u] Mulungu sanatuma Mwana wace ku dziko lapansi, kuti akaweruze dziko lapansi, koma kuti dziko lapansi likapulumutsidwe ndi Iye. 18 [z] Wokhulupirira Iye saweruzidwa; wosakhulupira waweruzidwa ngakhale tsopano, cifukwa sanakhulupirira dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu. 19 Koma ciweruziro ndi ici, kuti [b] kuunika kunadza ku dziko lapansi, ndipo anthu anakonda mdima koposa kuunika; pakuti nchito zao zinali zoipa. 20 Pakuti [c] yense wakucita zoipa adana nako kuunika, ndipo sakudza kwa kuunika, kuti zingatsutsidwe nchito zace. 21 Koma wocita coonadi adza kukuunika,

[a] Agal. 6. 15
Tito 3. 5
1 Petr. 1. 23
[b] Yoh. 4. 2
[c] Aroma 8. 9
1 Akor. 15 50
[d] Mat. 3. 5, 6
[e] Mat. 14. 3
[f] Yoh. 1. 7, 15, 27, 34
[g] Yoh. 6. 52, 60
[h] Yak. 1. 17
[i] Mat. 11. 27
Yoh. 1. 18
v. 32
[j] Yoh. 1. 20, 23, 27
[k] Aefeso 5. 25, 27
[l] Yoh. 6. 33, 38, 51, 62
[m] Mat. 3. 11
[n] Num. 21. 9
Yoh. 8. 28
[o] Yoh. 8. 23
[p] v. 16, 36
[r] Aroma 5. 8
1 Yoh. 4. 9
[s] v. 11
[t] Aroma 3. 4
1 Yoh. 5. 10
[u] Luka 9. 56
1 Yoh. 4. 14
[v] Yoh. 7. 16
[w] Yoh. 1. 16
[y] Mat. 11. 27
,, 28. 18
[z] Yoh. 5. 24
[a] v. 15, 16
1 Yoh. 5. 10
[b] Yoh. 1. 4, 5, 9, 10, 11
[c] Aefeso 5. 13
[d] Yoh. 3. 22, 26

kuti nchito zace zionekere kuti zinacitidwa mwa Mulungu.

### *Yohane acitanso umboni za Yesu.*

22 Zitapita izi anadza Yesu ndi akuphunzira ace ku dziko la Yudeya; ndipo pamenepo anatsotsa nao pamodzi, [b] nabatiza. 23 Ndipo Yohane analinkubatiza m'Ainoni pafupi pa Salemu, cifukwa panali madzi ambiri pamenepo; ndipo analinkufikako anthu, [d] nalinkubatizidwa. 24 Pakuti [e] Yohane sanaikidwe m'ndende. 25 Pamenepo padauka kufunsana mwa ophunzira ace a Yohane ndi Myuda za mayeretsedwe. 26 Ndipo anadza kwa Yohane, nati kwa iye, Rabi, Iye amene anali ndi inu tsidya lija la Yordano, [f] amene munamcitira umboni, taonani yemweyu abatiza, ndipo anthu onse alinkudza kwa Iye. 27 Yohane anayankha nati, [h] Munthu sakhoza kulandira kanthu, ngati sikapatsidwa kwa iye kocokera Kumwamba. 28 Inu nokha mundicitira umboni, kuti ndinati, [j] Sindine Kristu, koma kuti ndiri wotumidwa m'tsogolo mwace mwa Iye. 29 [k] Iye amene ali naye mkwatibwi ali mkwati, koma mnzace wa mkwatiyo, wakuimirira ndi kumvera iye, akondwera kwakukuru cifukwa ca mau a mkwatiyo; cifukwa cace cimwemwe canga cimene cakwanira. 30 [m] Iyeyo ayenera kukula, koma ine ndicepe.

31 [o] Iye wocokera Kumwamba ali woposa onse; iye amene ali wa dziko lapansi ali wa dziko lapansi, nalankhula za dziko lapansi: Iye wocokera Kumwamba ali woposa onse. 32 [s] Cimene anaciona, nacimva acita umboni wa ici comwe; ndipo kulibe munthu alandira umboni wace. 33 [t] Iye amene analandira umboni wace anaikapo cizindikilo cace kuti Mulungu ali woona. 34 Pakuti [v] Iye amene Mulungu anamtuma alankhula mau a Mulungu; pakuti [w] sapatsa Mzimu ndi muyeso. 35 [y] Atate akonda Mwana, nampatsa zinthu zonse m'dzanja lace. 36 [a] Iye amene akhulupirira Mwanayo ali nao moyo wosatha; koma iye amene sakhulupirira Mwanayo sadzaona moyo, koma mkwiyo wa Mulungu ukhala pa iye.

## 4 *Mkazi wa ku Samariya.*

Cifukwa cace pamene Ambuye anadziwa kuti Afarisi adamva kuti Yesu anayesa anthu ophunzira, [d] nawabatiza koposa Yohane 2 (angakhale

Yesu sanabatiza yekha koma ophu-
nzira ace), 3 anacokera ku Yudeya,
namukanso ku Galileya. 4 Ndipo
anayenera kupita pakati pa Samariya.
5 Cifukwa cace anadza ku mudzi wa
Samariya, dzina lace Sukari, pafupi
pa kadziko [d] kamene Yakobo adapatsa
mwana wace Yosefe; 6 ndipo pame-
nepo panali citsime ca Yakobo. Ndi-
po Yesu, popeza analema ndi ulendo
wace motero anakhala pacitsime.
7 Kunali ngati ora lacisanu ndi ci-
modzi. Kunadza mkazi woturuka
m'Samariya kudzatunga madzi. Yesu
ananena naye, Undipatse ine ndimwe.
8 Pakuti ophunzira ace adacoka ku-
nka kumudzi kuti akagule cakudya.
9 Pamenepo mkazi wa m'Samariya
ananena ndi Iye, Bwanji Inu, muli
Myuda, mupempha kwa ine kumwa,
ndine mkazi Msamariya? [h] (pakuti
Ayuda sayenderana nao Asamariya).
10 Yesu anayankha nati kwa iye,
Ukadadziwa mtulo wa Mulungu, ndi
Iye amene alinkunena ndi iwe, Undi-
patse ine ndimwe; [j] ukadapempha
Iye, ndipo akadakupatsa madzi amoyo.
11 Mkaziyo ananena ndi Iye, Ambuye
mulibe cotungira madzi, ndi citsime
ciri cakuya; ndipo mwatenga kuti
madzi amoyo? 12 kodi muli wamku-
ru ndi atate wathu Yakobo amene
anatipatsa ife citsimeci, namwamo
iye yekha, ndi ana ace, ndi zoweta
zace? 13 Yesu anayankha nati kwa
iye, Yense wakumwako madzi awa
adzamvanso ludzu; 14 koma [k] iye
wakumwa madzi amene Ine ndidza-
mpatsa sadzamva ludzu nthawi zonse;
koma madzi amene Ine ndidzampa-
tsa adzakhala mwa iye kasupe wa
madzi otumphukira ku moyo wosa-
tha. 15 Mkaziyo ananena kwa Iye,
Ambuye, ndipatseni madzi amene, kuti
ndisamve ludzu, kapena ndisadze
kuno kudzatunga. 16 Yesu ananena
kwa iye, Muka, kamuitane mwa-
muna wako, nudze kuno. 17 Mkazi
anayankha nati kwa Iye, Ndiribe
mwamuna. Yesu ananena naye, Wa-
nena bwino, kuti mwamuna ndiribe;
18 pakuti wakhala nao amuna asa-
nu; ndipo iye amene ukhala naye
tsopano sali mwamuna wako; ici
wanena zoona. 19 Mkazi ananena
ndi Iye, Ambuye, ndizindikira kuti
[n] muli Mneneri. 20 Makolo athu
analambira [o] m'phiri ili; ndipo inu
munena, kuti [p] m'Yerusalemu muli
malo oyenera kulambiramo anthu.
21 Yesu ananena naye, Tamvera
Ine, mkazi iwe, [r] kuti ikudza nthawi,
imene simudzalambira Atate kapena
m'phiri ili, kapena m'Yerusalemu.
22 Inu [a] mulambira cimene simuci-
dziwa; ife tilambira cimene ticidzi-
wa; pakuti [b] cipulumutso cicokera
kwa Ayuda. 23 Koma ikudza ntha-
wi, ndipo tsopano iripo, imene [c] ola-
mbira oona adzalambira Atate mu-
mzimu ndi m'coonadi; pakuti Atate
afuna otere akhale olambira ace.
24 [e] Mulungu ndiye mzimu; ndipo
omlambira Iye ayenera kumlambira
mumzimu ndi m'coonadi. 25 Mkazi
ananena ndi Iye, Ndidziwa kuti
Mesiya adza (wochedwa Kristu):
[f] akadzadza Iyeyu, adzatiuza zonse.
26 Yesu ananena naye, [g] Ine wakula-
nkhula nawe ndine amene.
27 Ndipo pamenepo anadza ophu-
nzira ace; nazizwa kuti analinku-
lankhula ndi mkazi; koma panalibe
wina anati, Mufuna ciani? kapena,
mulankhula naye ciani? 28 Pa-
menepo mkazi anasiya mtsuko wace,
namuka kumudzi, nanena ndi anthu,
29 Tiyeni, mukaone munthu, [i] amene
anandiuza zinthu ziri zonse ndina-
zicita: ameneyu sali Kristu nanga?
30 Anaturuka iwo m'mudzi ndipo
analinkudza kwa Iye.

### Za masika ndi anchito.

31 Pa mphindikati iyi ophunzira
ace anampempha Iye, ndi kunena,
Rabi, idyani. 32 Koma Iye anati kwa
iwo, Ine ndiri naco cakudya cimene
inu simucidziwa. 33 Cifukwa cace
ophunzira ananena wina ndi mnzace,
Kodi pali wina anamtengera Iye ka-
nthu kakudya? 34 Yesu ananena
nao, [l] Cakudya canga ndico kuti ndi-
cite cifuniro ca Iye amene ananditumа
Ine, ndi kutsiriza nchito yace. 35 Kodi
simunena inu, kuti, Yatsala miyezi
inai, ndipo kudza kumweta? Onani
ndinena kwa inu, Kwezani maso
anu, nimuyang'ane m'minda, [m] kuti
mwayera kale kufikira kumweta.
36 Wakumweta alandira kulipira,
nasonkhanitsira cobala ku moyo wo-
satha; kuti wofesayo akakondwere
pamodzi ndi womwetayo. 37 Pakuti
m'menemo conenaco ciri coona, Wo-
fesa ndi wina, womweta ndi winanso.
38 Ine ndinatuma inu kukamweta
cimene simunagwirirapo nchito: ena
anagwira nchito, ndipo inu mwalowa
nchito yao.

### Yesu ndi Asamariya.

39 Ndipo m'mudzi muja anthu
Asamariya ambiri anamkhulupirira
Iye [s] cifukwa ca mau a mkazi, wocita
umboniyo, kuti, Anandiuza ine zinthu

[a] 2 Maf. 17. 29
[b] Aroma 9. 4, 5
[c] Afil. 3. 3
[d] Yos. 24. 32
[e] 2 Akor. 3. 17
[f] v. 29, 39
[g] Marko 14. 61, 62
[h] Mac. 10. 28
[i] v. 25
[j] Yes. 44. 3
[k] Yoh. 6. 35; „ 7. 38
[l] Yoh. 6. 38
[m] Mat. 9. 37
[n] Luka 7. 16
[o] Yos. 8. 33; Ower. 9. 7
[p] 1 Maf. 9. 3
[r] Malaki 1. 11
[s] v. 29





ziri zonse ndinazicita. 40 Cifukwa
cace pamene Asamariya anadza kwa
Iye, anamfunsa akhale nao; ndipo
anakhala komweko masiku awiri.
41 Ndipo ambiri oposa anakhulupira
cifukwa ca mau ace; 42 ndipo ana-
nena kwa mkazi, kuti, Tsopano siti-
khulupira cifukwa ca kulankhula
kwako: pakuti [b] tamva tokha, ndipo
tidziwa kuti Mpulumutsi wa dziko
lapansi ndi Iyeyu ndithu.

### Yesu aciritsa mwana wa Mkuru.

43 Koma atapita masiku awiriwo
anacoka komweko kunka ku Galileya.
44 Pakuti Yesu mwini anacita
umboni kuti, [c] Mneneri alibe ulemu
m'dziko la kwao. 45 Cifukwa cace
pamene anadza ku Galileya, Agalileya
anamlandira Iye, [e] atakaona zonse
zimene anazicita m'Yerusalemu pa-
phwando; pakuti iwonso ananka
kuphwando.
46 Cifukwa cace Yesu anadzanso
ku Kana wa m'Galileya, [g] kumene
anasandutsa madzi vinyo. Ndipo
kunali mkulu wina wa mfumu,
mwana wace anadwala m'Kapernao.
47 Iyeyu, pamene anamva kuti Yesu
wacokera ku Yudeya nafika ku
Galileya, ananka kwa Iye, nampe-
mpha kuti atsike kukaciritsa mwa-
na wace; pakuti anali pafupi imfa.
48 Pamenepo Yesu anati kwa iye,
[i] Ngati simuona zizindikilo ndi zozi-
zwa, simudzakhulupira. 49 Mkuluyo
ananena kwa Iye, Ambuye, tsikani
asanafe mwana wanga. 50 Yesu
ananena naye, Muka, mwana wako
ali ndi moyo. Munthuyo anakhulu-
pirira mau amene Yesu anatero naye,
namuka. 51 Ndipo m'mene anali-
kutsika, akapolo ace anakomana naye,
nanena, kuti, Mwana wanu ali ndi
moyo. 52 Cifukwa cace anawafunsa
ora lace anayamba kuciralo. Pame-
nepo anati kwa iye, kuti, Dzulo, ora
lacisanu ndi ciwiri malungo ana-
msiya. 53 Cifukwa cace atateyo ana-
dziwa kuti ndi ora lomwelo limene
Yesu anati kwa iye, Mwana wako ali
ndi moyo; ndipo anakhulupira iye
yekha ndi a pa banja lace onse.
54 Ici ndi cizindikilo caciwiri Yesu
anacita, atacokera ku Yudeya, ndi
kulowa m'Galileya.

## 5 Yesu aciritsa wopuwala ku tamanda la Betesda.

Zitapita izi panali phwando la
Ayuda; ndipo [n] Yesu anakwera ku-
nka ku Yerusalemu.
2 Koma pali thamanda m'Yerusa-
lemu [a] pa cipata ca nkhosa, lochedwa
m'Cihebri Betesda, liri ndi makumbi
asanu. 3 M'menemo munagona kha-
mu lalikuru la anthu odwala, akhu-
ngu, opunduka miyendo, opuwala.
5 Koma panali munthu wina apo, ali
m'kudwala kwace zaka makumi atatu
kudza zisanu ndi zitatu. 6 Yesu,
pakuona ameneyo alikugona, ndipo
anadziwa kuti anatero nthawi yai-
kuru pamenepo, ananena naye, Ufuna
kuciritsidwa kodi? 7 Wodwalayo
anayankha, Ambuye, ndiribe wondi-
bvika ine m'thamanda, pali ponse
madzi abvundulidwa; koma m'mene
ndirinkudza ine, wina atsika ndisa-
natsike ine. 8 Yesu ananena naye,
[d] Tauka, yalula mphasa yako, nu-
yende. 9 Ndipo pomwepo munthuyo
anacira, nayalula mphasa yace, na-
yenda.
Koma [f] tsiku lomwelo linali la
Sabata. 10 Cifukwa cace Ayuda ana-
nena kwa wociritsidwayo, Ndi Sabata,
ndipo [h] sikuloledwa kwa iwe kuya-
lula mphasa yako. 11 Koma iyeyu
anayankha iwo, Iye amene anandi-
ciritsa, yemweyu anati kwa ine, Ya-
lula mphasa yako, nuyende. 12 Ana-
mfunsa, Munthuyo ndani wonena ndi
iwe, Yalula mphasa yako, nuyende?
13 Koma wociritsidwayo sanadziwa
ngati ndani; pakuti Yesu anacoka
kacetecete, popeza panali anthu au-
nyinji m'malo muja. 14 Zitapita izi
Yesu anampeza m'kacisi, nati kwa
iye, Taona, waciritsidwa; [j] usaci-
mwenso, kuti cingakugwere coipa
coposa. 15 Munthuyo anacoka, nauza
Ayuda, kuti ndiye Yesu amene ada-
mciritsa.

### Yesu adziulula kuti ali Mwana wa Mulungu.

16 Ndipo cifukwa ca ici Ayuda ana-
londalonda Yesu, popeza anacita izo
dzuwa la Sabata. 17 Koma Yesu
anayankha iwo, [k] Atate wanga ama-
gwira nchito kufikira tsopano, Inenso
ndigwira nchito. 18 Cifukwa ca ici
Ayuda anaonjeza kufuna kumupha,
si cifukwa ca kuswa dzuwa la Sabata
kokha, komatu amachanso Mulungu
Atate wace wa Iye yekha; [l] nadzi-
yesera wolingana ndi Mulungu.
19 Pamenepo Yesu anayankha
nati kwa iwo, Indetu, indetu, ndinena
kwa inu, [m] sakhoza Mwana kucita
kanthu pa yekha, koma cimene aona
Atate acicita, ndico. Pakuti zimene
Iye azicita, zomwezo Mwananso azi-
cita momwemo. 20 Pakuti [o] Atate

[a] Neh. 3. 1
[b] Yoh. 17. 8; 1 Yoh. 4. 14
[c] Mat. 13. 57
[d] Mat. 9. 6; Marko 2. 11; Luka 5. 24
[e] Yoh. 2. 23
[f] Yoh. 9. 14
[g] Yoh. 2. 7-9
[h] Eks. 20. 10; Mat. 12. 2; Marko 2. 24; Luka 6. 2
[i] 1 Akor. 1. 22
[j] Mat. 12. 45; Yoh. 8. 11
[k] Yoh. 9. 4
[l] Afil. 2. 6
[m] v. 30; Yoh. 12. 49
[n] Yoh. 2. 13
[o] Mat. 3. 17

akonda Mwana, namuonetsa zonse
asicita yekha: ndipo adzamuonetsa
nchito zoposa izi, kuti mukazizwe.
21 Pakuti monga Atate aukitsa aku-
fa, nawapatsa moyo, [b] momwemonso
Mwana apatsa moyo iwo amene Iye
afuna. 22 Pakuti Atate saweruza
munthu ali yense, koma [d] anapereka
kuweruza konse kwa Mwana; 23 kuti
onse akalemekeze Mwana, monga
alemekeza Atate. [f] Wosalemekeza
Mwana salemekeza Atate amene ana-
mtuma Iye. 24 Indetu, indetu, ndi-
nena kwa inu, kuti [g] iye wakumva
mau anga, ndi kukhulupirira Iye
amene ananditumа Ine, ali nao moyo
wosatha, ndipo salowa m'kuweruza,
koma [i] wacokera kuimfa, nalowa
m'moyo. 25 Indetu, indetu, ndinena
kwa inu, kuti ikudza nthawi, ndipo
iripo tsopano, imene [j] akufa adzamva
mau a Mulungu; ndipo iwo akumva
adzakhala ndi moyo. 26 Pakuti mo-
nga Atate ali ndi moyo mwa Iye
yekha, momwemonso anapatsa kwa
Mwana kukhala ndi moyo mwa Iye
yekha; 27 ndipo [m] anampatsa Iye
mphamvu ya kucita mlandu, pakuti
ali Mwana wa munthu. 28 Musa-
zizwe ndi ici, kuti ikudza nthawi,
[n] imene onse ali m'manda adzamva
mau ace, 29 nadzaturukira, [o] amene
adacita zabwino, kukuuka kwa moyo;
koma amene adacita zoipa kukuuka
kwa kuweruza.
30 [r] Sindikhoza kucita kanthu kwa
Ine ndekha; monga momwe ndimva
ndiweruza; ndipo maweruzidwe anga
ali olungama; cifukwa kuti [s] sindi-
tsata cifuniro canga, koma cifuniro
ca Iye wondituma Ine. 31 Ngati ndi-
cita umboni wa Ine ndekha, umboni
wanga suli woona. 32 [u] Wocita
umboni wa Ine ndi wina; ndipo ndi-
dziwa kuti umboni umene Iye andicitira
Ine uli woona. 33 Inu munatuma kwa
Yohane, ndipo [w] iye anacitira umboni
coonadi. 34 Ndipo Ine sindilandira
umboni kwa munthu: koma ndinena
izi, kuti inu mukapulumutsidwe.
35 Iyeyo anali nyali yoyaka ndi yo-
wala; ndipo inu munafuna kuko-
ndwera m'kuunika kwace kanthawi.
36 Koma Ine ndiri nao umboni
woposa wa Yohane; pakuti [z] nchito
zimene Atate anandipatsa ndizitsirize,
nchito zomwezo ndizicita zindici-
tira umboni, kuti Atate ananditumа
Ine. 37 Ndipo Atate wondituma-
yo, [b] Iyeyu wandicitira Ine umboni.
Simunamva mau ace konse, kape-
na maonekedwe ace simunaona.
38 Ndipo mulibe mau ace okhala
mwa inu; cifukwa kuti amene
Iyeyu anatuma, inu simumkhu-
lupirira ameneyo. 39 [a] Musanthula
m'malembo, popeza muyesa kuti
momwemo muli nao moyo wosatha;
ndipo akundicitira Ine umboni ndi
iwo omwewo; 40 ndipo [c] simufuna
kudza kwa Ine, kuti mukhale nao
moyo. 41 [e] Ulemu sindiulandira kwa
anthu. 42 Koma ndikudziwani inu,
kuti mulibe cikondi ca Mulungu
mwa inu nokha. 43 Ndadza Ine
m'dzina la Atate wanga, ndipo
simundilandira Ine; akadza wina
m'dzina lace la iye mwini, iyeyu
mudzamlandira. 44 Mungathe inu
bwanji kukhulupira, [h] popeza mula-
ndira ulemu wina kwa mnzace; ndipo
ulemu wakucokera kwa Mulungu
yekha simuufuna? 45 Musayesa
kuti Ine ndidzakunenezani inu kwa
Atate; [k] pali wakukunenezani, ndiye
Mose, amene inu mumtama. 46 Pa-
kuti, mukadakhulupirira Mose, mu-
kadakhulupirira Ine; [l] pakuti iyeyu
analembera za Ine. 47 Koma ngati
simukhulupirira malembo a iyeyu,
mudzakhulupirira bwanji mau anga?

## 6 *Yesu acurukitsa mikate.*

(Mat. 14. 13-21. Marko 6. 30-44.
Luka 9. 10-17.)

[p] Zitapita izi anacoka Yesu kunka
ku tsidya lija la nyanja ya Galileya,
ndiyo ya Tiberiya. 2 Ndipo khamu
lalikuru la anthu linamtsata Iye,
cifukwa anaona zizindikilo zimene
anacita pa odwala. 3 Koma Yesu
anakwera kuphiri, nakhala pansi ko-
mweko pamodzi ndi akuphunzira ace.
4 Ndipo [t] Paskha, phwando la Ayuda,
unayandikira. 5 Pamenepo Yesu,
[v] pokweza maso ace, ndi kuona kuti
khamu lalikuru lirinkudza kwa Iye,
ananena kwa Filipo, Tidzagula kuti
mikate kuti adye awa? 6 Koma
ananena ici kuti amuyese; pakuti
anadziwa yekha cimene adzacita.
7 Filipo anayankha Iye, [y] Mikate ya
marupiya atheka mazana awiri sii-
kwanira iwo, kuti yense atenge pa-
ng'ono. 8 Mmodzi wa akuphunzira
ace, Andreya, mbale wace wa Simoni
Petro, ananena ndi Iye, 9 Pali mnya-
mata pano, amene ali nayo mikate
isanu yabarele, ndi tinsomba tiwiri;
koma [a] nanga izi zifikira bwanji ambiri
otere? 10 Nati Yesu, Akhalitseni
anthu pansi. Ndipo panali udzu wa-
mbiri pamalopo. Pamenepo amu-
ñawo anakhala pansi, kuwerenga
kwao monga zikwi zisanu. 11 Po-
mwepo Yesu anatenga mikateyo;
ndipo pamene adayamika, anagawira

[a] Luka 24. 27 v. 46 — [b] Luka 7. 14, 15 „ 8. 54, 55 — [c] Yoh. 1. 11 „ 3. 19 — [d] Mat. 11. 27 — [e] v. 34 — [f] 1 Yoh. 2. 23 — [g] Yoh. 3. 16, 18 — [h] Yoh. 12. 43 Aroma 2. 29 — [i] 1 Yoh. 3. 14 — [j] v. 28 — [k] Aroma 2. 12 — [l] Gen. 3. 15 „ 49. 10 Mac. 26. 22 — [m] v. 22 — [n] v. 25 1 Akor. 15. 52 — [o] Mat. 25. 32, 33, 46 — [p] Mat. 14. 15 — [r] v. 19 — [s] Yoh. 4. 34 — [t] Lev. 23. 5, 7 — [u] Mat. 3. 17 — [v] Mat. 14. 14 — [w] Yoh. 1. 15, 19, 27, 32 — [y] Num. 11. 21, 22 — [z] Yoh. 10. 25 — [a] 2 Maf. 4. 43 — [b] Mat. 17. 5





iwo akukhala pansi; momwemonso
ndi tinsomba, monga momwe iwo
anafuna. 12 Ndipo pamene ada-
khuta, Iye ananena kwa akuphunzira
ace, Sonkhanitsani makombo kuti
kasatayike kanthu. 13 Pomwepo
anasonkhanitsa, nadzaza mitanga
khumi ndi iwiri ndi makombo a mi-
kate isanuyo yabarele, amene anatsalira
anadyawo. 14 Cifukwa cace, anthu,
poona cizindikilo cimene anacita, ana-
nena, kuti, [d] Ameneyo ndiye mneneri
ndithu wakudzayo m'dziko lapansi.
15 Pamenepo Yesu, pozindikira
kuti alikufuna kudza kudzamgwira
Iye, kuti amlonge ufumu, anaco-
kanso kunka kuphiri pa yekha.

### *Yesu ayenda panyanja.*

(Mat. 14. 22-34. Marko 6. 45, 46.)

16 Koma [h] pofika madzulo, aku-
phunzira ace anatsikira kunyanja;
17 ndipo pamene adalowa m'nga-
lawa, analikuoloka nyanja kunka
ku Kapernao. Ndipo kutada pame-
nepo, koma Yesu asanadze kwa iwo.
18 Ndipo nyanja inalikuuka cifukwa
ca mphepo yaikulu yakuombako.
19 Ndipo pamene adapalasa monga
mastadiya makumi awiri ndi asanu
kapena makumi atatu, anaona Yesu
alikuyenda panyanja, ndi kuyandi-
kira ngalawa; ndipo anacita mantha.
20 Koma Iye ananena nao, Ndine;
musaope. 21 Pamenepo analola ku-
mlandira m'ngalawa; ndipo pomwepo
ngalawayo inafika kumtunda kumene
analikunkako.

### *Yesu mkate wamoyo wa okhu-lupirira.*

22 M'mawa mwace khamu la
anthu limene linaima tsidya lija la
nyanja linaona kuti palibe ngalawa
yina koma imodzi, ndi kuti Yesu
sanalowa pamodzi ndi akuphunzira
ace m'ngalawamo, koma akuphunzira
ace adacoka pa okha; 23 koma zina-
cokera ngalawa zina ku Tiberiya,
pafupi pa malo pomwe adadyapo
mkate m'mene Yesu adayamika;
24 cifukwa cace pamene khamu la
anthu linaona kuti palibe Yesu, ndi
akuphunzira ace palibe, iwo okha
analowa m'ngalawazo nadza ku
Kapernao, alikufuna Yesu. 25 Ndipo
pamene anampeza Iye tsidya lina la
nyanja, anati kwa Iye, Rabi, munadza
kuno liti? 26 Yesu anayankha iwo
nati, Indetu, indetu, ndinena ndi inu,
Mundifuna Ine, si cifukwa munaona
zizindikilo, koma cifukwa munadya
mkate, nimunakhuta. 27 Gwirani
nchito si cifukwa ca cakudya cimene
citayika koma [a] ca cakudya cimene
citsalira ku moyo wosatha, cimene
Mwana wa munthu adzakupatsani
inu; pakuti [b] ameneyo Atate, ndiye
Mulungu, adamlembera cizindikilo.
28 Pamenepo anati kwa Iye, Ticite
ciani, kuti ticite nchito za Mulungu?
29 Yesu anayankha nati kwa iwo,
[c] Nchito ya Mulungu ndi iyi, kuti
mukhulupirire Iye amene Iyeyo ana-
mtuma. 30 Cifukwa cace anati kwa
Iye, Ndipo [e] mucita cizindikilo canji,
kuti tione ndi kukhulupirira Inu?
mucita ciani? 31 [f] Atate athu ana-
dya mana m'cipululu; monga kwa-
lembedwa, Mkate wocokera m'mwa-
mba anawapatsa iwo kudya. 32 Ci-
fukwa cace Yesu anati kwa iwo,
Indetu, indetu, ndinena kwa inu, [g] Si
Mose amene anakupatsani inu mkate
wa Kumwamba; koma Atate wanga
akupatsani inu mkate woona wa
Kumwamba. 33 Pakuti mkate wa
Mulungu ndiye wakutsika kucokera
Kumwamba ndi kupatsa moyo kwa
dziko lapansi. 34 Pamenepo anati
kwa Iye, Ambuye, tipatseni ife mkate
umene nthawi zonse. 35 Yesu anati
kwa iwo, [i] Ine ndine mkate wamoyo;
iye amene adza kwa Ine sadzamva
njala, ndi [j] iye amene akhulupirira
Ine sadzamva ludzu nthawi zonse.
36 Koma ndinati kwa inu, kuti mu-
ngakhale mwandiona, simukhulupi-
rira. 37 [k] Cinthu conse cimene ana-
ndipatsa Ine Atate cidzadza kwa Ine;
ndipo [l] wakudza kwa Ine sindidza-
mtaya iye kunja. 38 Pakuti ndina-
tsika Kumwamba, [m] si kuti ndicite
cifuniro canga, koma cifuniro ca Iye
amene ananditumа Ine. 39 Koma
cifuniro ca Iye amene ananditumа
Ine ndi ici, kuti [n] za ici conse Iye
anandipatsa Ine ndisatayeko kanthu,
koma ndiciukitse tsiku lomariza.
40 Pakuti cifuniro ca Atate wanga
ndi ici, kuti [o] yense wakuyang'ana
Mwana, ndi kukhulupirira Iye, akhale
nao moyo wosatha; ndipo Ine ndi-
dzamuukitsa iye tsiku lomariza.
41 Cifukwa cace Ayuda anang'u-
ng'udza za Iye, cifukwa anati, [p] Ine
ndine mkate wotsika Kumwamba.
42 Ndipo iwo ananena, [r] Si Yesu
uyu, mwana wa Yosefe, atate wace
ndi amai wace tiwadziwa? Anena
bwanji tsopano, kuti, Ndinatsika Ku-
mwamba? 43 Yesu anayankha nati
kwa iwo, Musang'ung'udze wina ndi
mnzace. 44 [s] Kulibe mmodzi akhoza
kudza kwa Ine koma ngati Atate
wonditumа Ine amkoka iye; ndipo

[a] v. 54 — [b] Mat. 3. 17 — [c] 1 Yoh. 3. 23 — [d] Deut. 18. 15, 18 — [e] Mat. 12. 38 — [f] Eks. 16. 15 Sal. 78. 24, 25 — [g] Eks. 16. 15 Sal 78. 24, 25 — [h] Mat. 14. 23 — [i] v. 48, 58 — [j] Yoh. 4. 14 „ 7. 37 — [k] v. 45 — [l] Yoh. 10. 28, 29 2. Tim 2. 19 1 Yoh. 2. 19 — [m] Mat. 26. 39 Yoh. 5. 30 — [n] Yoh. 10. 28 „ 17. 12 — [o] v. 27, 47, 54 Yoh. 3. 15, 16 — [p] v. 33, 50 — [r] Mat. 13. 55 — [s] v. 65

Ine ndidzamuukitsa iye tsiku loma-
riza. 45 [a] Calembedwa mwa aneneri,
Ndipo adzakhala onse ophunzitsidwa
ndi Mulungu. [b] Yense amene ada-
mva kwa Atate, naphunzira, adza
kwa Ine. 46 [d] Sikuti munthu wina
waona Atate, koma [e] Iye amene ali
wocokera kwa Mulungu, ameneyo
waona Atate. 47 Indetu, indetu, ndi-
nena ndi inu, [g] Iye wokhulupira ali
nao moyo wosatha. 48 [h] Ine ndine
mkate wamoyo. 49 [i] Makolo anu
adadya m'cipululu, ndipo adamwalira.
50 [j] Mkate wotsika Kumwamba ndi
uwu, kuti munthu akadyeko ndi
kusamwalira. 51 [k] Mkate wamoyo
wotsika Kumwamba Ndine amene.
Ngati munthu wina akadyako mkate
umene, adzakhala ndi moyo kosatha.
Inde, ndipo [m] mkate umene ndidza-
patsa Ine, ndiwo thupi langa, ukhale
moyo wa dziko lapansi.
52 Pamenepo Ayuda anatetana
wina ndi mnzace ndi kunena,
Akhoza bwanji ameneyu kutipatsa
ife kudya thupi lace? 53 Cifukwa
cace Yesu anati kwa iwo, Indetu,
indetu, ndinena ndi inu, [o] Ngati simu-
kudya thupi la Mwana wa munthu ndi
kumwa mwazi wace, mulibe moyo
mwa inu nokha. 54 [s] Iye wakudya
thupi langa ndi kumwa mwazi wanga
ali nao moyo wosatha; ndipo Ine
ndidzamuukitsa iye tsiku lomariza.
55 Pakuti thupi langa ndi cakudya
ndithu, ndi mwazi wanga ndi caku-
mwa ndithu. 56 Iye wakudya thupi
langa ndi kumwa mwazi wanga
[t] akhala mwa Ine ndi Ine mwa iye.
57 Monga Atate wamoyo ananditu-
ma Ine, ndipo Inenso ndiri ndi moyo
cifukwa ca Atate; momwemo wondi-
dya Ine iyeyu adzakhala ndi moyo
cifukwa ca Ine. 58 [w] Mkate wotsika
Kumwamba ndi umenewu: si monga
makolowo, anadya namwalira; iye
wakudya mkate umene adzakhala ndi
moyo nthawi zonse. 59 Izi ananena
m'sunagoge, pakuphunzitsa m'Kape-
rnao.

*Ophunzira ambiri aleka kutsata Yesu.*

60 [z] Pamenepo ambiri a akuphu-
nzira ace, pakumva izi, anati, Mau
awa ndi osautsa; akhoza kumva awa
ndani? 61 Koma Yesu podziwa
mwa yekha kuti akuphunzira ace
alikung'ung'udza cifukwa ca ici,
anati kwa iwo, Ici mukhumudwa
naco? 62 [c] Nanga bwanji ngati mu-
kaona Mwana wa munthu alikukwera
kumene anali kale lomwe? 63 [d] Wo-
patsa moyo ndi mzimu; thupi si-
lithandiza konse. Mau amene nda-
lankhula ndi inu ndiwo mzimu, ndi
moyo. 64 Koma [e] pali ena mwa
inu amene sakhulupira. Pakuti Yesu
anadziwa poyamba amene ali osa-
khulupira, ndi amene adzampereka.
65 Ndipo ananena, [f] Cifukwa ca ici
ndinati kwa inu, kuti palibe munthu
angathe kudza kwa Ine, koma ngati
kupatsidwa kwa iye ndi Atate.

*Cibvomerezo ca Petro.*
(Mat. 16. 13-20. Marko 8. 27-30.
Luka 9. 18-21.)

66 [l] Pa ici ambiri a akuphunzira
ace anabwerera m'mbuyo, ndipo
sanayenda-yendanso ndi Iye. 67 Ci-
fukwa cace Yesu anati kwa khumi
ndi awiriwo, Nanga inunso mufuna
kucoka? 68 Simoni Petro anamya-
nkha Iye, Ambuye, tidzamuka kwa
yani? Inu muli nao mau a moyo
wosatha. 69 Ndipo [n] ife tikhulupi-
rira, ndipo tidziwa kuti Inu ndinu
Woyera wa Mulungu. 70 Yesu
anayankha iwo, [p] Kodi sindinakusa-
nkhani khumi ndi awiri, ndipo mwa
inu [r] mmodzi ali mdierekezi? 71 Ko-
ma adanena za Yudase, mwana wa
Simoni Isikariote, pakuti iye ndiye
amene akampereka Iye, ali mmodzi
wa khumi ndi awiri.

7 *Abale a Yesu sambvomereza.*

Ndipo zitapita izi Yesu anayenda-
yenda m'Galileya; pakuti sanafuna
kuyendayenda m'Yudeya, [u] cifukwa
Ayuda anafuna kumupha Iye. 2 Ko-
ma phwando la Ayuda, [v] phwando
la misasa, linayandikira. 3 Cifukwa
cace abale ace anati kwa Iye, Cokani
pano, mumuke ku Yudeya, kuti aku-
phunzira anunso akapenye nchito
zanu zimene mucita. 4 Pakuti palibe
munthu acita kanthu mobisika, na-
funa yekha kukhala poyera. Ngati
mucita izi, dzionetsereni eni nokha
kwa dziko lapansi. 5 Pakuti anga-
khale abale ace sanakhulupirira Iye.
6 Cifukwa cace Yesu ananena nao,
[y] Nthawi yanga siinafike; koma
nthawi yanu yakonzeka masiku onse.
7 [a] Dziko lapansi silingathe kudana
ndi inu; koma Ine lindida popeza
Ine ndilicitira umboni, kuti nchito
zace ziri zoipa. 8 Kwerani inu ku-
nka kuphwando; sindikwera Ine ku
phwando ili tsopano apa; [b] pakuti
nthawi yanga siinakwanire. 9 Ndipo
m'mene adanena nao zimenezi ana-
khalabe m'Galileya.

a Yes. 54. 13
b v. 37
c v. 66, 71
d Yoh. 1. 18
„ 5. 37
e Mat. 11. 27
f v. 44, 45
g Yoh. 3. 15, 16, 36
h v. 35
i v. 31
j v. 33
k v. 33
l v. 60
m Ahebr. 10. 5, 10
n Mat. 16. 16
o Mat. 26. 26, 28
p Luka 6. 13
r Yoh. 13. 27
s v. 27, 63
t 1 Yoh. 3. 24
u Yoh. 5. 16, 18
v Lev. 23. 34
w v. 49-51
y Yoh. 8. 20
z v. 66
a Yoh. 15. 19
b v. 6
c Marko 16. 19
Yoh. 3. 13
Mac. 1. 9
d 2 Akor. 3. 6





*Yesu aphunzitsa m'Kacisi. Ayesa kumgwira.*

10 Koma pamene abale ace ada-
kwera kunka kuphwando, pomwepo
Iyenso anakwera, si poonekera, ko-
ma monga mobisalika. 11 Pomwepo
Ayuda analikumfuna Iye paphwando,
nanena, Ali kuti uja? 12 Ndipo
[d] kunali kung'ung'udza kwambiri za
Iye m'makamu a anthu; ena ana-
nena, kuti, Ali wabwino; koma ena
ananena, Iai, koma asoceretsa khamu
la anthuwo. 13 Cinkana anatero
panalibe munthu analankhula za Iye
poyera, cifukwa ca kuopa Ayuda.
14 Koma pamene padafika pakati
pa phwando, Yesu anakwera nalowa
m'kacisi, naphunzitsa. 15 Cifukwa
cace Ayuda anazizwa, nanena, [f] Ame-
neyu adziwa bwanji zolemba, wosa-
phunzira? 16 Pamenepo Yesu ana-
yankha iwo, nati, [h] Ciphunzitso canga
siciri canga, koma ca Iye amene
ananditurna Ine. 17 Ngati munthu
ali yense afuna kucita cifuniro cace,
adzazindikira za ciphunzitsoco, ngati
cicokera kwa Mulungu, kapena ndi-
lankhula zocokera kwa Ine ndekha.
18 Iye wolankhula zocokera kwa iye
yekha afuna ulemu wa mwini yekha.
Iye wakufuna ulemu wa Iye amene
anamtuma, yemweyu ali woona, ndi-
po mwa Iye mulibe cosalungama.
19 [j] Si Mose kodi anakupatsani inu
cilamulo, ndipo kulibe mmodzi mwa
inu acita cilamulo? [k] Mufuna ku-
ndipha cifukwa ninji? 20 Khamu
la anthu linayankha, [l] Muli ndi ciwa-
nda: afuna ndani kukuphani Inu?
21 Yesu anayankha nati kwa iwo,
Ndinacita nchito imodzi, ndipo mu-
zizwa monse. 22 [o] Cifukwa ca ici
Mose anakupatsani inu mdulidwe (si
kuti ucokera kwa Mose, koma [r] kwa
makolo); ndipo mudula munthu
tsiku la Sabata. 23 Ngati munthu
alandira mdulidwe tsiku la Sabata,
kuti cilamulo ca Mose cingapasuli-
dwe; kodi mundikwiyira Ine, [t] cifu-
kwa ndamciritsadi munthu tsiku la
Sabata? 24 Musaweruze monga ma-
onekedwe, koma weruzani ciweruziro
colungama.
25 Pamenepo ena a iwo a ku Yeru-
salemu ananena, Kodi suyu amene
afuna kumupha? 26 ndipo taona
amalankhula poyera, ndipo sanena
kanthu kwa Iye. Kapena kodi akuru
adziwa ndithu kuti ndiye Kristu ame-
neyo? 27 Koma [y] ameneyo tidziwa
uko acokera: koma Kristu pamene
akadzadza, palibe mmodzi adzadziwa
uko acokera. 28 Pamenepo Yesu
anapfuula m'kacisi, alikuphunzitsa
ndi kunena, Mundidziwa Ine, ndiponso
mudziwa uko ndicokera; ndipo
[a] sindinadza Ine ndekha, koma Iye
wondituma Ine amene inu simumdzi-
wa, ali woona. 29 [b] Ine ndimdziwa
Iye; cifukwa ndiri wocokera kwa
Iye, nanditurna Ine Iyeyu. 30 [c] Pa-
menepo anafuna kumgwira Iye;
koma palibe wina anamgwira ku-
manja, cifukwa nthawi yace siina-
fike. 31 Koma [e] ambiri a m'khamu
la anthu anakhulupirira Iye; ndi-
po ananena, Pamene Kristu akadza
kodi adzacita zizindikilo zambiri zo-
posa zimene adazicita ameneyo?
32 Afarisi anamva khamu la anthu
ling'ung'udza zimenezi za Iye; ndi-
po ansembe akulu ndi Afarisi ana-
tuma anyamata kuti akamgwire Iye.
33 Pamenepo Yesu anati, [g] Katsala
kanthawi ndiri ndi inu, ndipo ndimu-
ka kwa Iye wondituma Ine. 34 [i] Mu-
dzafunafuna Ine, osandipeza; ndipo
pomwe ndiri Ine, inu simungathe
kudzapo. 35 Cifukwa cace Ayuda
anati mwa iwo okha, Adzanka kuti
uyu kuti ife sitikampeza Iye? kodi
adzamuka kwa Ahelene obalalikawo,
ndi kuphunzitsa Ahelene? 36 Mau
awa amene ananena ndi ciani, Mudza-
ndifunafuna osandipeza Ine: ndipo
pomwe ndiri Ine, inu simungathe
kudzapo?

*Yesu aneneratu za Mzimu Woyera.*

37 Koma [m] tsiku lomariza, laliku-
rulo la phwando, Yesu anaimirira
napfuula, ndi kunena, [n] Ngati pali
munthu akumva ludzu, adze kwa Ine,
namwe. 38 Iye wokhulupirira Ine,
monga cilembo cinati, [p] Mitsinje ya
madzi amoyo idzayenda, kuturuka
m'kati mwace. 39 Koma [s] ici anati
za Mzimu, amene iwo akukhulupirira
Iye anati adzalandire; pakuti Mzimu
panalibe pamenepo, cifukwa Yesu sa-
nalemekezedwa panthawi pomwepo.

*Anthu atsutsana za Iye.*

40 Pamenepo ena a khamulo pa-
kumva mau awa, ananena, [u] Mnene-
riyo ndi uyu ndithu. 41 Ena ana-
nena, [v] Uyu ndi Kristu. Koma ena
ananena, Kodi Kristu adza kuturuka
m'Galileya. 42 [w] Kodi sicinati cile-
mbo kuti Kristu adza kuturuka
mwa mbeu ya Davide, ndi kucokera
ku Betelehemu, kumudzi kumene
kunali Davide? 43 [z] Kudakhala tso-
no kusiyana m'khamulo cifukwa ca

a Yoh. 5. 43
b Mat. 11. 27
c Marko 11. 18
d Yoh. 9. 16
e Yoh. 8. 30
f Mat. 13. 54
g Yoh. 13. 33
h Yoh. 8. 28
i Yoh. 13. 33
j Eks. 24. 3
k Mat. 12. 14
l Yoh. 8. 48, 52
m Lev. 23. 36
n Yes. 55. 1
Cibv. 22. 17
o Lev. 12. 3
p Yoh. 4. 14
r Gen. 17. 10
s Yes. 44. 3
Yow. 2. 28
t Yoh. 5. 8, 9, 16
u Deut. 18. 15, 18
v Yoh. 4. 42
w Yer. 23. 5
Mika 5. 2
y Mat. 13. 55
z v. 12

Iye. 44 Koma [a] ena mwa iwo anafuna
kumgwira Iye; koma palibe munthu
anamgwira kumanja.
45 Pamenepo anyamatawo ana-
dza kwa ansembe akulu ndi Afarisi;
ndipo iwowa anati kwa iwo, Simu-
namtenga Iye bwanji? 46 Anya-
matawo anayankha, [c] Nthawi yonse
palibe munthu analankhula cote-
ro. 47 Pamenepo Afarisi anayankha
iwo, Kodi mwasokeretsedwa inunso?
48 [d] Kodi wina wa akuru anakhulu-
pirira Iye, kapena wa Afarisi?
49 Koma khamu ili losadziwa
cilamulo, likhala lotemberereredwa.
50 [f] Nikodemo ananena kwa iwo,
amene uja adadza kwa Iye kale, ali
mmodzi wa iwo, 51 Kodi cilamulo
cathu ciweruza munthu, osayamba
kumva iye, ndi kuzindikira cimene
acita? 52 Anayankha nati kwa iye,
Kodi iwenso uli woturuka m'Gali-
leya? Santhula, nuone kuti m'Gali-
leya sanauka mneneri. 53 Ndipo
anamuka munthu yense ku nyumba
yace.

## 8 *Za mkazi wacigololo.*

Koma Yesu anamuka ku phiri la
Azitona. 2 Koma mamawa ana-
dzanso kukacisi, ndipo anthu onse
anadza kwa Iye; ndipo m'mene ana-
khala pansi anawaphunzitsa. 3 Koma
alembi ndi Afarisi anabwera naye kwa
Iye mkazi wogwidwa m'cigololo, ndi-
po pamene anamuimika iye pakati,
4 ananena kwa Iye, Mphunzitsi,
mkazi uyu wagwidwa alimkucita cigo-
lolo. 5 Koma m'cilamulo [n] Mose
anatilamulira, tiwaponye miyala otere.
Cifukwa cace Inu munena ciani za
iye? 6 Koma ici ananena kuti amu-
yese Iye, kuti akhale naco comneneza
Iye. Koma Yesu, m'mene adawe-
rama pansi analemba pansi ndi cala
cace. 7 Koma pamene anakhala-
khala alikumfunsabe Iye, anawera-
muka, nati kwa iwo, [p] Amene mwa
inu ali wopanda cimo, ayambe ku-
mponya mwala. 8 Ndipo m'mene
adaweramanso analemba ndi cala
cace pansi. 9 Koma iwo, m'mene
adamva, anaturukamo amodzi amo-
dzi, kuyambira akulu, kufikira otsi-
riza; ndipo Yesu anatsala yekha, ndi
mkazi, alikuima pakati. 10 Koma
Yesu pamene adaweramuka, anati
kwa iye, Mkazi iwe, ali kuti ajawa?
Palibe munthu anakutsutsa kodi?
11 Koma iye anati, Palibe, Ambuye.
Ndipo Yesu anati, [v] Inenso sindiku-
tsutsa iwe; pita; kuyambira tsopano
usacimwenso.

*Yesu wotumidwa ndi Atate.*

12 Pamenepo Yesu analankhula-
nso nao, nanena, [b] Ine ndine kuunika
kwa dziko lapansi; iye wonditsata
Ine sadzayenda mumdima, koma
adzakhala nako kuunika kwa moyo.
13 Cifukwa cace Afarisi anati kwa
Iye, Mucita umboni wa Inu nokha;
umboni wanu suli woona. 14 Ana-
yankha Yesu nati kwa iwo, Ndinga-
khale ndicita umboni wa Ine ndekha
umboni wanga uli woona; cifukwa
ndidziwa kumene ndinacokera ndi
kumene ndimukako; koma [e] inu
simudziwa kumene ndicokera, ndi
kumene ndimukako. 15 Inu mu-
weruza monga mwa thupi; [g] Ine
sindiweruza munthu. 16 Ndipo ngati
ndiweruza Ine, ciweruziro canga ciri
coona; [h] pakuti sindiri pa ndekha,
koma Ine ndi Atate amene anandi-
tuma Ine. 17 Inde [i] kudalembedwa
m'cilamulo canu kuti umboni wa
anthu awiri uli woona. 18 Ine ndine
wakucita umboni wa Ine ndekha,
ndipo [j] Atate amene ananditunia Ine
acita umboni wa Ine. 19 Cifu-
kwa cace ananena ndi Iye, Ali kuti
Atate wanu? Yesu anayankha,
[k] Simudziwa kapena Ine, kapena
Atate wanga; [l] mukadadziwa Ine,
mukadadziwanso Atate wanga.
20 Mau awa analankhula m'nyu-
mba ya cuma ca Mulungu pophu-
nzitsa m'kacisi; ndipo palibe munthu
anamgwira Iye, [m] pakuti nthawi yace
siinafike.
21 Pamenepo anatinso kwa iwo;
Ndimuka Ine, ndipo [o] mudzandifuna,
ndipo m'cimo lanu mudzafa: ku-
mene ndimukako Ine, simudziwa ku-
dza inu. 22 Cifukwa cace Ayuda
ananena, Kodi adzadzipha yekha, pa-
kuti ananena, Kumene ndimukako
Ine, simudziwa inu kudza? 23 Ndipo
ananena nao, Inu ndinu ocokera
pansi; Ine ndine wocokera Kumwa-
mba; [r] inu ndinu a dziko lino la-
pansi; sindiri Ine wa dziko lino
lapansi. 24 Cifukwa cace ndinati
kwa inu, kuti [s] mudzafa m'macimo
anu, pakuti [t] ngati simukhulupirira
kuti Ine ndine, mudzafa m'macimo
anu. 25 Pamenepo ananena kwa Iye,
Ndinu yani? Yesu anati kwa iwo,
Cimene comwe ndidalankhulanso ndi
inu kuyambira paciyambi. 26 Ndiri
nazo zambiri zakulankhula ndi za-
kuweruza za inu; koma wonditurna
Ine ali woona; ndipo [u] zimene nda-
zimva kwa Iye, zomwezo ndilankhula
kwa dziko lapansi. 27 Sanazindikira
iwo kuti analikunena nao za Atate.

[a] v. 30
[b] Yoh. 1. 4, 5, 9
" 9. 5
[c] Mat. 7. 29
[d] Yoh. 12. 42
[e] Yoh. 9. 29
[f] Yoh. 3. 1, 2
[g] Yoh. 3. 17
[h] v. 29
[i] Deut. 17. 6
[j] Yoh. 5. 37
[k] v. 55
[l] Yoh. 14. 7
[m] Yoh. 7. 30
[n] Lev. 20. 10
[o] Yoh. 7. 34
[p] Deut. 17. 7
Aroma 2. 1
[r] Yoh. 3. 31
[s] v. 21
[t] Marko 16. 16
[u] Yoh. 15. 15
[v] Yoh. 3. 17





28 Cifukwa cace Yesu anati, [a] Pa-
mene mutadzamkweza Mwana wa
munthu, pomwepo mudzazindikira
kuti Ine ndine, ndipo sindicita ka-
nthu kwa Ine ndekha, koma monga
anandiphunzitsa Atate, ndilankhula
izi. 29 Ndipo wondituma Ine ali ndi
Ine; [c] sanandisiya Ine pa ndekha;
[d] cifukwa ndicita Ine zimene zi-
mkondweretsa Iye nthawi zonse.
30 Pakulankhula Iye zimenezi, ambiri
anakhulupirira Iye.
31 Cifukwa cace Yesu ananena kwa
Ayuda aja adakhulupirira Iye, Ngati
mukhala inu m'mau anga, muli aku-
phunzira anga ndithu; 32 ndipo
mudzazindikira coonadi, ndipo [g] co-
onadi cidzakumasulani. 33 Anamya-
nkha iye, [i] Tiri mbeu ya Abrahamu,
ndipo sitinakhala akapolo a munthu
nthawi iri yonse; munena bwanji,
Mudzayesedwa aufulu? 34 Yesu ana-
yankha iwo, nati, Indetu, indetu,
ndinena kwa inu kuti [k] yense waku-
cita cimo ali kapolo wa cimolo.
35 Koma kapolo sakhala m'nyumba
nthawi yonse; mwana ndiye akhala
nthawi yonse. 36 Cifukwa cace [l] ngati
Mwana adzakuyesani inu aufulu, mu-
dzakhala mfulu ndithu. 37 Ndidziwa
kuti muli mbeu ya Abrahamu; koma
mufuna kundipha Ine, cifukwa mau
anga alibe malo mwa inu. 38 [n] Zime-
ne ndinaona Ine kwa Atate, ndila-
nkhula; ndipo inunso muchita cimene
mudamva kwa atate wanu. 39 Ana-
yankha nati kwa iye, Atate wathu
ndiye Abrahamu. Yesu ananena nao,
[p] Ngati muli ana a Abrahamu, muka-
dacita nchito za Abrahamu. 40 Koma
tsopano mufuna kundipha Ine, ndine
munthu amene ndinalankhula ndi
inu coonadi, [s] cimene ndinamva kwa
Mulungu; ici Abrahamu sanacita.
41 Inu mucita nchito za atate wanu.
Anati kwa Iye, Sitinabadwa ife m'ci-
gololo; tiri naye Atate mmodzi ndiye
Mulungu. 42 Yesu anati kwa iwo,
[v] Mulungu akadakhala Atate wanu,
mukadakonda Ine; pakuti Ine ndina-
turuka, ndi kucokera kwa Mulungu;
pakuti sindinadza kwa Ine ndekha,
koma Iyeyu ananditurna Ine. 43 Si-
muzindikira malankhulidwe anga ci-
fukwa ninji? Cifukwa simungathe
kumva mau anga. 44 [w] Inu muli oco-
kera mwa atate wanu mdierekezi,
ndipo zolakalaka zace za atate wanu
mufuna kucita. Iyeyu anali wamba-
nda kuyambira paciyambi, ndipo
sanaima m'coonadi, pakuti mwa iye
mulibe coonadi. Pamene alankhula
bodza, alankhula za mwini wace;
pakuti ali wabodza, ndi atate wace
wa bodza. 45 Koma Ine, cifukwa
ndinena coonadi, simukhulupirira Ine.
46 Ndani mwa inu anditsutsa Ine za
cimo? Ngati ndinena coonadi, si-
mundikhulupirira Ine cifukwa ninji?
47 [b] Iye wocokera kwa Mulungu amva
zonena za Mulungu; inu simumva
cifukwa cakuti simuli a kwa Mulungu.
48 Ayuda anayankha nati kwa Iye,
Kodi sitinenetsa kuti Inu ndinu Msa-
mariya, ndipo [e] muli ndi ciwanda?
49 Yesu anayankha, Ndiribe ciwanda
Ine; koma ndilemekeza Atate wanga,
ndipo inu mundipeputsa. 50 Koma
[f] Ine sinditsata ulemerero wanga;
alipo woutsata ndi wakuweruza.
51 Indetu, indetu, ndinena ndi inu,
[h] Munthu akasunga mau anga, sadza-
ona imfa nthawi yonse. 52 Ayuda
anati kwa Iye, Tsopano tazindikira
kuti muli ndi ciwanda. [j] Abrahamu
anamwalira, ndi aneneri; ndipo Inu
munena, Munthu akasunga mau anga,
sadzalawa imfa ku nthawi yonse.
53 Kodi Inu ndinu wamkulu ndi
atate wathu Abrahamu, amene ana-
mwalira? ndipo aneneri anamwa-
lira: mudziyesera nokha muli yani?
54 Yesu anayankha, Ngati Ine ndi-
dzilemekeza ndekha, ulemerero wanga
uli cabe; [m] Atate wanga ndiye wondi-
lemekeza Ine; amene munena za Iye,
kuti ndiye Mulungu wanu; 55 ndipo
[o] inu simunamdziwa Iye; koma Ine
ndimdziwa Iye; ndipo ngati ndinena,
kuti sindimdziwa Iye, ndidzakala
wonama modzimodzi inu; koma ndi-
mdziwa Iye, ndipo ndisunga mau ace.
56 [r] Atate wanu Abrahamu anako-
ndwera kuona tsiku langa; ndipo
anaona, nasangalala. 57 Ayuda pa-
menepo anati kwa Iye, Simuna-
fikire zaka makumi asanu, ndipo
munaona Abrahamu kodi? 58 Yesu
anati kwa iwo, Indetu, indetu, ndinena
kwa inu, asanayambe kukhala Abra-
hamu ndipo [t] Ine ndiripo. 59 Pame-
nepo [u] anatola miyala kuti amponye
Iye; koma Yesu anabisala, naturuka
m'kacisi.

## 9 *Aciritsidwa munthu wosaona cibadwire.*

Ndipo popita, anaona munthu ali
wosaona cibadwire. 2 Ndipo aku-
phunzira ace anamfunsa Iye, nanena,
Rabi, anacimwa ndani, ameneyo,
kapena atate wace ndi amace, kuti
anabadwa wosaona? 3 Yesu ana-
yankha, Sanacimwa ameneyo, kapena
atate wace ndi amace; koma [y] kuti
nchito za Mulungu zikaonetsedwe mwa
iye. 4 [z] Tiyenera kugwira nchito za

[a] Yoh. 3. 14
" 12. 32, 34
[b] Yoh. 10. 26, 27
[c] v. 16
[d] Yoh. 4. 34
[e] Yoh. 7. 20
[f] Yoh. 7. 18
[g] Aroma 6. 14, 18, 22
[h] Yoh. 11. 26
[i] Lev. 25. 42
v. 39
[j] Ahebr. 11. 13
[k] Aroma 6. 16-20
[l] Aroma 8. 2
[m] Yoh. 16. 14
" 17. 1
[n] Yoh. 3. 32
[o] Yoh. 7. 28, 29
[p] Aroma 9. 7
[r] Ahebr. 11. 13
[s] v. 26
[t] Yoh. 17. 5, 24
Akol. 1. 17
[u] Yoh. 10. 31
[v] 1 Yoh. 5. 1
[w] Mat. 13. 38
1 Yoh. 3. 8
[y] Yoh. 11. 4
[z] Yoh. 4. 34
" 17. 4

Iye wondituma Ine, pokhala pali
msana; ukudza usiku pamene palibe
munthu angakhoze kugwira nchito.
5 Pakukhala Ine m'dziko lapansi,
[a] ndiri kuunika kwa dziko lapansi.
6 Pamene ananena izi, [c] analabvula
pansi, nakanda thope ndi malobvuwo,
napaka thopelo m'maso, 7 nati kwa
iye, Muka, kasambe [d] m'thamanda la
Siloamu (ndilo losandulika, Wotu-
midwa). Pamenepo anacoka, [e] na-
samba, nabwera alikuona. 8 Cifukwa
cace anzace ndi iwo adamuona kale,
kuti anali wopemphapempha, ana-
nena, Kodi si uyu uja wokhala ndi
kupemphapempha? 9 Ena ananena,
kuti, Ndiyeyu; ena ananena, lai, koma
afanana naye. Iyeyu anati, Ndine
amene. 10 Pamenepo ananena ndi
iye, Nanga maso ako anatseguka
bwanji? 11 Iyeyu anayankha, [f] Mu-
nthuyo wochedwa Yesu anakanda
thope, napaka m'maso mwanga, nati
kwa ine, Muka ku Siloamu kasambe;
cifukwa cace ndinacoka, ndipo m'mene
ndinasamba ndinapenya. 12 Ndipo
anati kwa iye, Ali kuti Iyeyo?
Anena, Sindidziwa ine.

13 Anapita naye amene anali wo-
saona kale kwa Afarisi. 14 Ko-
ma tsikulo ndi la Sabata limene
Yesu anakanda thope, namtsegulira
iye maso ace. 15 Pamenepo ndipo
Afarisi anamfunsanso, umo ana-
penyera. Ndipo anati kwa iwo,
Anapaka thope m'maso mwanga,
ndinasamba, ndipo ndipenya. 16 Ena
pamenepo mwa Afarisi ananena,
[j] Munthu uyu sacokera kwa Mulu-
ngu, cifukwa sasunga Sabata. Koma
ena ananena, [k] Munthu ali wocimwa
akhoza bwanji kucita zizindikilo zo-
tere? Ndipo panali kutsutsana mwa
iwo. 17 Pamenepo ananenanso kwa
wosaonayo, Iwe unenanji za Iye,
popeza anakutsegulira maso ako?
Koma iye anati, [m] Ali Mneneri. 18 Ci-
fukwa cace Ayuda sanakhulupirira za
iye, kuti anali wosaona, napenya,
kufikira kumene adaitana atate wace
ndi amace a iye wopenya; 19 nawa-
funsa iwo, nanena, Kodi uyu ndi
mwana wanu, amene inu munena
kuti anabadwa wosaona? 20 Ndipo
apenya bwanji tsopano? Atate wace
ndi amace anayankha nati, Tidziwa
kuti uyu ndi mwana wathu, ndi kuti
anabadwa wosaona; 21 koma siti-
dziwa umo apenyera tsopano; ka-
pena sitimdziwa amene anamtsegulira
pamaso pace; mumfunse iye; ali
wamsinkhu; adzalankhula mwini za
iye yekha. 22 Izi ananena atate
wace ndi amace, [r] cifukwa anaopa

a v. 34
b Yoh. 1.5, 9
,, 12. 35, 36, 46
c Marko 7. 33
Marko 8. 23
d Neh. 3. 15
e 2 Maf. 5. 14
f v. 6, 7
g Yoh. 8. 14
h Sal. 66. 18
Yer. 11. 11
Mika 3. 4
i Yoh. 3. 2
j Mat. 12. 2
k v. 33
l Mat. 16. 15, 16
m Yoh. 6. 14
n Yoh. 4. 26
o Yoh. 5. 22, 27
p Yoh. 15. 22, 24
r Yoh. 7. 13

Ayuda; pakuti Ayuda adapangana
kale, kuti ngati munthu ali ye-
nse adzambvomereza Iye kuti ndiye
Kristu, [a] akhale woletsedwa m'suna-
goge. 23 Cifukwa ca ici atate wace
ndi amace anati, Ali wamsinkhu;
mumfunse iye. 24 Pamenepo ana-
muitana kaciwiri munthuyo amene
anali wosaona, nati kwa iye, Leme-
keza Mulungu; tidziwa kuti munthuyo
ali wocimwa. 25 Pamenepo iyeyu
anayankha, Ngati ali wocimwa, sindi-
dziwa; cinthu cimodzi ndicidziwa,
pokhala ndinali wosaona, tsopano ndi-
penya. 26 Cifukwa cace anati kwa
iye, Anakucitira iwe ciani? anaku-
tsegulira iwe maso bwanji? 27 Iye
anayanka iwo, Ndinakuuzani kale,
ndipo simunamva; mufuna kumva-
nso bwanji? kodi inunso mufuna
kukhala akuphunzira ace? 28 Ndipo
anamlalatira iye, nati, Ndiwe wo-
phunzira wa Iyeyu; ife ndife aku-
phunzira a Mose. 29 Tidziwa ife kuti
Mulungu analankhula ndi Mose;
koma [g] sitidziwa kumene acokera
ameneyo. 30 Munthuyu anayankha
nati kwa iwo, Pakuti cozizwa ciri
m'menemo, kuti inu simudziwa ku-
meme acokera, ndipo ananditsegulira
maso anga. 31 [h] Tidziwa kuti Mu-
lungu samvera ocimwa. Koma ngati
munthu ali yense akhala wopembedza
Mulungu nacita cifuniro cace, amvera
ameneyo. 32 Kuyambira paciyambi
sikunamveka kuti wina anatsegulira
maso munthu wosaona cibadwire.
33 [i] Ngati uyu sanacokera kwa Mu-
lungu, sakadakhoza kucita kanthu.
34 Anayankha nati kwa iye, Waba-
dwa iwe konse m'zoipa, ndipo iwe
utiphunzitse ife kodi? Ndipo ana-
mtaya kunja.

35 Yesu anamva kuti adamtaya
kunja; ndipo pakumpeza iye, anati,
[l] Kodi ukhulupirira Mwana wa Mulu-
ngu? 36 Iyeyu anayankha nati,
Ndipo ndani Iye, Ambuye, kuti ndi-
mkhulupirire Iye? 37 Yesu anati
kwa iye, Wamuona Iye, ndiponso
[n] wakulankhula ndi iwe ndi Iyeyo.
38 Koma iye anati, Ndikhulupirira
Ambuye; ndipo anamgwadira Iye.
39 Ndipo Yesu anati, [o] Kudzaweruza
ndadza Ine ku dziko lino lapansi, kuti
iwo osapenya apenye; ndi kuti iwo
akupenya akhale osaona. 40 Ndipo
Afarisi ena akukhala ndi Iye anamva
izi, nati kwa Iye, Kodi ifenso ndife
osaona? 41 Yesu anati kwa iwo,
[p] Mukadakhala osaona simukada-
khala nalo cimo; koma tsopano
munena, kuti, Tipenya: cimo lanu
likhala.





# 10 *Za Mbusa Wabwino.*

Indetu, indetu, ndinena ndi inu,
Iye wosalowa m'khola la nkhosa
pakhomo, koma akwerera kwina,
iyeyu ndiye wakuba ndi wolanda.
2 Koma iye wakulowera pakhomo,
ndiye mbusa wa nkhosa. 3 Iyeyu,
wapakhomo amtsegulira ndi nkhosa
zimva mau ace; ndipo aitana nkhosa
za iye yekha maina ao, nazitsogolera
kunja. 4 Pamene adaturutsa zonse
za iye yekha, azitsogolera; ndi
nkhosa zimtsata iye; cifukwa zi-
dziwa mau ace. 5 Koma mlendo
sizidzamtsata, koma zidzamthawa;
cifukwa sizidziwa mau a alendo.
6 Fanizo ili Yesu ananena kwa iwo;
koma sanazindikira zimene Yesu ana-
likulankhula nao.

7 Cifukwa cace Yesu ananenanso
nao, Indetu, indetu, ndinena ndi inu,
Ine ndine khomo la nkhosa. 8 Onse
amene anadza m'tsogolo mwa Ine ali
akuba, ndi olanda: koma nkhosa
sizinamva iwo. 9 [d] Ine ndine khomo;
ngati wina alowa ndi Ine, adzapulu-
mutsidwa, nadzalowa, nadzaturuka,
nadzapeza busa. 10 Siikudza mbala,
koma kuti ikabe, ndi kupha, ndi
kuononga. Ndadza Ine kuti akhale
ndi moyo, ndi kukhala nao wocuru-
ka. 11 [g] Ine ndine Mbusa Wabwino;
mbusa wabwino ataya moyo wace
cifukwa ca nkhosa. 12 Wolipidwa
amene sakhala mbusa, amene nkhosa
siziri zace za yekha, aona mmbulu
ulinkudza, [i] nasiya nkhosazo, natha-
wa; ndipo mmbulu uzikwatula, nu-
zibalalitsa; 13 cifukwa ali wolipidwa,
ndipo sasamala nkhosa. 14 Ine ndine
Mbusa Wabwino; ndipo [j] ndizindi-
kira zanga, ndi zanga zindizindikira
Ine, 15 [m] monga Atate andidziwa
Ine, ndi Ine ndimdziwa Atate; ndipo
[n] nditaya moyo wanga cifukwa ca
nkhosa. 16 Ndipo [o] nkhosa zina
ndiri nazo, zimene siziri za khola
ili; izinso ndiyenera kuzitenga, ndipo
zidzamva mau anga; ndipo [p] zidza-
khala gulu limodzi, mbusa mmodzi.
17 Cifukwa ca ici Atate andikonda
Ine, [s] cifukwa nditaya Ine moyo wa-
nga, kuti ndikautengenso. 18 Palibe
wina andicotsera uwu, koma ndiutaya
Ine ndekha. Ndiri nayo mphamvu
yakuutaya, ndi [u] mphamvu ndiri nayo
kuutenganso; lamulo ili ndinalandira
kwa Atate wanga.

19 Panakhalanso kutsutsana pa-
kati pa Ayuda cifukwa ca mau awa.
20 Koma ambiri mwa iwo ananena,
[w] Ali ndi ciwanda, nacita misala; mu-
kumva Iye bwanji? 21 Ena ananena,

a Yoh. 5. 36
b Yoh. 8. 47
c v. 4, 14
d Yoh. 14. 6
Aefeso 2. 18
e Yoh. 6. 37
,, 17. 11, 12
,, 18. 9
f Yoh. 17. 22
g Sal. 23.
Yes. 40. 11
Ahebr. 13. 20
h Yoh. 8. 59
i Zek. 11. 16, 17
j 2 Tim. 2. 19
k Yoh. 5. 18
l Sal. 82. 6
m Mat. 11. 27
n Yoh. 15. 13
o Yes. 56. 8
p Aefeso 2. 14
r Yoh. 8. 42
s Ahebr. 2. 9
t Yoh. 5. 36
v. 25
u Yoh. 2. 19
v Yoh. 14. 10, 11
w Yoh. 7. 20

Mau awa sali a munthu wogwidwa
ciwanda. Kodi ciwanda cikhoza ku-
mtsegulira maso wosaona?

## *Yesu adziulula ali Mwana wa Mulungu.*

22 Koma kunali phwando la ku-
konzetsanso m'Yerusalemu; nyengo-
yo ndi yacisanu. 23 Ndipo Yesu
analikuyendayenda m'kacisi, m'khu-
mbi la Solomo. 24 Pamenepo Ayuda
anamzungulira Iye, nanena ndi Iye,
Kufikira liti musinkhitsa-sinkhitsa
moyo wathu? ngati Inu ndinu Kristu,
tiuzeni momveka. 25 Yesu anaya-
nkha iwo, Ndakuuzani, ndipo simu-
khulupirira. [a] Nchitozi ndizicita Ine
m'dzina la Atate wanga, zimenezi
zindicitira umboni. 26 Koma [b] inu
simukhulupira, cifukwa simuli a mwa
nkhosa zanga. 27 [c] Nkhosa zanga
zimva mau anga, ndipo Ine ndizizindi-
kira, ndipo zinditsata Ine. 28 Ndipo
Ine ndizipatsa moyo wosatha; ndipo
[e] sizidzaononge ka ku nthawi yonse,
ndipo palibe munthu adzazikwatula
m'dzanja langa. 29 Atate wanga,
amene anandipatsa izo, ali wamkulu
ndi onse; ndipo palibe wina anga-
the kuzikwatula m'dzanja la Atate.
30 [f] Ine ndi Atate ndife amodzi.
31 [h] Ayuda anatolanso miyala kuti
amponye Iye. 32 Yesu anayankha
iwo, Ndakuonetsani inu nchito za-
bwino zambiri za kwa Atate; cifu-
kwa ca nchito iti ya izo mundiponya
miyala? 33 Ayuda anamyankha Iye,
Cifukwa ca nchito yabwino sitikupo-
nyani miyala, koma cifukwa ca
mwano; ndi kuti Inu, muli mu-
nthu, [k] mudziyesera nokha Mulungu
34 Yesu anayankha iwo, [l] Kodi siku-
lembedwa m'cilamulo canu, Ndinati
Ine, Muli milungu? 35 Ngati ana-
wacha milungu iwo amene mau a
Mulungu anawadzera (ndipo colemba
sicingathe kutyoka), 36 kodi inu mu-
nena za Iye, amene Atate anampa-
tula [r] namtuma ku dziko lapansi,
Ucita mwano; cifukwa ndinati,
Ndiri Mwana wa Mulungu? 37 Ngati
sindicita nchito za Atate wanga, mu-
sakhulupirira Ine. 38 Koma ngati
ndicita, mungakhale simukhulupi-
rira Ine, [t] khulupiririrani nchitozo;
kuti mukadziwe ndi kuzindikira kuti
[v] Atate ali mwa Ine, ndi Ine mwa
Atate. 39 Anafunanso kumgwira
Iye; ndipo anapulumuka m'dzanja
lao.

40 Ndipo anacoka kunkanso tsidya
lija la Yordano, kumalo kumene ku-
nali Yohane analikubatiza poyamba

paja; ndipo anakhala komweko.
41 Ndipo ambiri anadza kwa Iye;
nanena kuti, Sanacita cizindikilo
Yohane; koma [a] zinthu ziri zonse
Yohane ananena za iye zinali zoona.
42 Ndipo [b] ambiri anakhulupirira Iye
komweko.

## 11 *Ciukitso ca Lazaro.*

Koma panali munthu wodwala,
Lazaro wa ku Betaniya, wa m'mu-
dzi wa [c] Mariya ndi mbale wace
Marita. 2 Koma [d] ndiye Mariya uja
anadzoza Ambuye ndi mafuta onu-
nkhira bwino, napukuta mapazi ace
ndi tsitsi lace, amene mlongo wace
Lazaro anadwala. 3 Pamenepo alo-
ngo ace anatumiza kwa Iye, nanena,
Ambuye, onani, amene mumkonda
adwala. 4 Koma Yesu pamene ana-
mva, anati, Kudwala kumene sikuli
kwa imfa, koma [h] cifukwa ca uleme-
rero wa Mulungu, kuti Mwana wa
Mulungu alemekezedwe nako. 5 Ko-
ma Yesu anakonda Marita, ndi mbale
wace, ndi Lazaro. 6 Cifukwa cace
pamene anamva kuti anadwala ana-
khala pamenepo [j] pa malo pomwepo
masiku awiri. 7 Ndipo pambuyo pace
ananena kwa akuphunzira ace, Ti-
yeni tipitenso ku Yudeya. 8 Aku-
phunzira ananena ndi Iye, Ambuye,
[k] Ayuda analikufuna kukuponyani
miyala tsopano apa; ndipo munkanso
komweko kodi? 9 Yesu anayankha,
Kodi sikuli maora khumi ndi awiri
usana? Ngati munthu ayenda usa-
na sakhumudwa, cifukwa apenya
kuunika kwa dziko lino lapansi.
10 Koma [l] ngati munthu ayenda usi-
ku, akhumudwa, cifukwa mulibe ku-
unika mwa iye. 11 Izi anati, ndipo
zitatha izi ananena nao, Lazaro
bwenzi lathu [n] ali m'tulo; koma
ndimuka kukamuukitsa iye tulo tace.
12 Cifukwa cace akuphunzira ace
anati kwa Iye, Ambuye, ngati ali
m'tulo adzacira. 13 Koma Yesu
adanena za imfa yace; koma iwowa
anayesa kuti ananena za mpumulo
wa tulo. 14 Pamenepo Yesu anati kwa
iwo momweka, Lazaro wamwalira.
15 Ndipo ndikondwera cifukwa ca
inu kuti kunalibe Ine komweko,
cakuti mukakhulupire; koma ti-
yeni, tipite kwa iye. 16 Pamenepo
Tomasi, wochedwa Didimo, anati kwa
akuphunzira anzace, Tipite ifenso kuti
tikafere naye pamodzi.

17 Ndipo pamene Yesu anadza ana-
peza kuti pamenepo atakhala m'manda
masiku anai. 18 Koma Betaniya
anali pafupi pa Yerusalemu, nthawi

a Yoh. 3. 27-30
b Yoh. 8. 30
„ 11. 45
c Luka 10. 38, 39
d Yoh. 12. 2, 3
e Luka 14. 14
f Yoh. 6. 39, 40, 44
g Yoh. 6. 39, 40, 44
h Yoh. 9. 3
i Mat. 16. 16
Yoh. 6. 69
j Yoh. 10. 40
k Yoh. 10. 31
l Yoh. 12. 35
m v. 21
n Deut. 31. 16
Mat. 9. 24
Mac. 7. 60
1 Akor. 15. 18, 51
o Luka 19. 41
p Yoh. 9. 6

yace yonga ya mastadiya khumi ndi
asanu; 19 koma ambiri a mwa Ayu-
da adadza kwa Marita ndi Mariya,
kudzawatonthoza mtima pa mlongo
wao. 20 Pamenepo Marita, paku-
mva kuti Yesu alinkudza, anamuka
kukakomana ndi Iye; koma Mariya
anakhalabe m'nyumba. 21 Ndipo
Marita anati kwa Yesu, Ambuye, mu-
kadakhala kuno mlongo wanga sa-
kadafa. 22 Koma ngakhale tsopano
ndidziwa kuti zinthu ziri zonse mu-
kapempha Mulungu, adzakupatsani
Mulungu. 23 Yesu ananena naye,
Mlongo wako adzauka. 24 Marita
ananena ndi Iye, [e] Ndidziwa kuti
adzauka m'kuuka tsiku lomariza.
25 Yesu anati kwa iye, [f] Ine ndine
kuuka ndi moyo: wokhulupirira Ine,
angakhale amwalira, adzakhala ndi
moyo; 26 ndipo [g] yense wakukhala
ndi moyo, nakhulupirira Ine sadza-
mwalira nthawi yonse. Kodi ukhu-
lupirira ici? 27 Ananena ndi Iye,
Inde Ambuye; [i] ndakhulupirira ine
kuti Inu ndinu Kristu, Mwana wa
Mulungu, wakudza m'dziko lapansi.
28 Ndipo m'mene anati ici anacoka
naitana Mariya mbale wace m'tseri,
ndi kuti, Wafika Mphunzitsi, akuitana
iwe. 29 Koma iyeyo, pakumva, ana-
nyamuka msanga, nadza kwa Iye.
30 (Koma Yesu sanafike kumudzi,
koma anali pamalo pomwe Marita
adakomana ndi Iye.) 31 Pamenepo
Ayuda okhala naye m'nyumba, ndi
kumtonthoza iye, pakuona Mariya
ananyamuka msanga, naturuka, na-
mtsata iye, ndi kuyesa kuti amuka
kumanda kukalira komweko. 32 Po-
mwepo Mariya, pofika pamene panali
Yesu, m'mene anamuona Iye, anagwa
pa mapazi ace, nanena ndi Iye,
[m] Ambuye, mukadakhala kuno Inu,
mlongo wanga sakadamwalira. 33 Pa-
menepo Yesu, pakumuona iye aliku-
lira, ndi Ayuda akumperekeza iye
alikulira, anadzuma mumzimu, na-
bvutika mwini, 34 nati, Mwamuika
iye kuti? Ananena ndi Iye, Ambuye,
tiyeni, mukaone. 35 [o] Yesu analira.
36 Cifukwa cace Ayuda ananena,
Taonani, anamkondadi! 37 Koma
ena mwa iwo anati, Kodi uyu [p] wotse-
gulira maso wosaona uja, sanakhoza
kodi kucita kuti sakadafa amene-
yunso. 38 Pamenepo Yesu, ndi ku-
dzumanso mwa Iye yekha anadza
kumanda. Koma panali phanga,
ndipo mwala unaikidwa pamenepo.
39 Yesu ananena, Cotsani mwala.
Marita, mlongo wace wa womwali-
rayo, ananena ndi Iye, Ambuye, ada-
yamba kununkha: pakuti wagona





masiku anai. 40 Yesu ananena naye,
Kodi sindinati kwa iwe, kuti, ngati
ukhulupira, [b] udzaona ulemerero wa
Mulungu? 41 Pomwepo anacotsa
mwala. Koma Yesu anakweza maso
ace kupenya kumwamba nati, Atate,
ndiyamika Inu kuti munamva Ine.
42 Koma ndadziwa Ine kuti muma-
ndimva Ine nthawi zonse; koma [c] ci-
fukwa ca khamu la anthu alikuimi-
rira pozungulira ndinanena ici, kuti
akhulupire kuti Inu munandituma
Ine. 43 Ndipo m'mene adanena izi,
anapfuula ndi mau akuru, Lazaro,
turuka. 44 Ndipo womwalirayo ana-
turuka womangidwa miyendo ndi
manja ndi nsaru za kumanda; ndi
[f] nkhope yace inazingidwa ndi mlezo.
Yesu ananena nao, Mmasuleni iye,
ndipo mlekeni amuke.

45 Cifukwa cace [g] ambiri a mwa
Ayuda amene anadza kwa Mariya,
m'mene anaona cimene anacita, ana-
khulupirira Iye. 46 Koma ena a mwa
iwo anamuka kwa Afarisi, nawauza
zimene Yesu adazicita.

### *Afarisi apangana za kupha Yesu.*

47 [i] Pamenepo ansembe akulu ndi
Afarisi anasonkhanitsa akulu, nanena,
Titani ife? cifukwa munthu uyu
acita zizindikilo zambiri. 48 Ngati
timleka Iye kotero, onse adzakhulu-
pirira Iye; ndipo adzadza Aroma
nadzacotsa malo athu ndi mtundu
wathu. 49 Koma [k] wina mmodzi wa
mwa iwo, Kayafa, wokhala mkulu
wa ansembe caka comweco anati
kwa iwo, Simudziwa kanthu konse
inu, 50 [m] kapena simuganiza kuti nko-
koma kwa inu kuti munthu mmodzi
afere anthu, ndi kuti mtundu wonse
usaonongeke. 51 Koma ici sananena
kwa iye yekha; koma pokhala mkulu
wa ansembe caka comweco ananenera
kuti Yesu akadzafera mtunduwo;
52 ndipo [o] si cifukwa ca mtunduwo
wokha ai, koma kuti akasonkhanitse
pamodzi ana a Mulungu akubalalikawo.
53 Cifukwa cace, kuyambira tsiku
lomwelo anapangana kuti amuphe Iye.
54 Cifukwa cace Yesu [r] sanayenda-
yendanso poonekera mwa Ayuda,
koma anacokapo kunka ku dziko
loyandikira cipululu, kumudzi dzina
lace Efraimu; nakhala komweko
pamodzi ndi akuphunzira ace.
55 Koma Paskha wa Ayuda unali
pafupi; ndipo ambiri anakwera
kunka ku Yerusalemu kucoka ku
miraga, usanafike Paskha, kukadzi-
yeretsa iwo okha. 56 Pamenepo

a Yoh. 7. 11
b v. 4, 23
c Yoh. 12. 30
d Yoh. 11. 1, 43
e Yoh. 11. 2
f Yoh. 20. 7
g Yoh. 10. 42
h Yoh. 11. 2
i Sal. 2. 2
Mat. 26. 3
j Yoh. 13. 29
k Yoh. 18. 14
l Mat. 26. 11
m Yoh. 18. 14
n Yoh. 11. 43, 44
o Yes. 49. 6
Aefeso 2. 14-17
p Yoh. 11. 45
r Yoh. 7. 1
s Mat. 21. 8
t Sal. 118. 26

[a] analikumfuna Yesu, nanena wina
ndi mnzace poimirira iwo m'kacisi,
Muyesa bwanji inu, sadzadza kuphwa-
ndo kodi? 57 Koma ansembe akulu
ndi Afarisi adalamulira, kuti, munthu
wina akadziwa pokhala Iye, aulule,
kuti akamgwire Iye.

## 12 *Mariya adzoza mapazi a Yesu.*

(Mat. 26. 6-13. Marko 14. 3-9.)

Pomwepo anatsala masiku asanu
ndi limodzi usanafike Paskha, Yesu
anadza ku Betaniya [d] kumene kunali
Lazaro, amene Yesu adamuukitsa
kwa akufa. 2 Ndipo [e] anamkonzera
Iye cakudya komweko; ndipo Marita
anatumikira; koma Lazaro anali
mmodzi wa iwo akuseama pacaku-
dya pamodzi ndi Iye. 3 Pamenepo
[h] Mariya m'mene adatenga muyeso
umodzi wa mafuta onunkhira bwino a
nardo a mtengo wace wapatali, ana-
dzoza mapazi a Yesu, napukuta ma-
pazi ace ndi tsitsi lace; ndipo nyumba
inadzazidwa ndi mnunkho wace wa
mafutawo. 4 Koma Yudase Isikari-
ote, mmodzi wa akuphunzira ace,
amene adzampereka Iye, ananena,
5 Nanga mafuta onunkhira awa sana-
gulitsidwa cifukwa ninji ndi marupiya
atheka mazana atatu, ndi kupatsidwa
kwa osauka? 6 Koma ananena ici si
cifukwa analikusamalira osauka, koma
cifukwa anali mbala, ndipo [j] pokhala
nalo thumba, amaba zoikidwamo.
7 Pamenepo Yesu anati, Mleke iye,
pakuti anacisungira ici tsiku la kuiki-
dwa kwanga. 8 Pakuti [l] osauka muli
nao pamodzi ndi inu nthawi zonse;
koma simuli ndi Ine nthawi zonse.

9 Pamenepo khamu lalikuru la
Ayuda linadziwa kuti ali pomwepo;
ndipo anadza, si cifukwa ca Yesu
yekha, koma kuti adzaone Lazaro,
[n] amene adamuukitsa kwa akufa.
10 Koma ansembe akulu anapanga-
na kuti akaphe Lazaronso; 11 pakuti
[p] ambiri a Ayuda anacoka cifukwa ca
iye, nakhulupirira Yesu.

### *Yesu alowa m'Yerusalemu.*

(Mat. 21. 1-12. Marko 11. 1-10.
Luka 19. 29-38.)

12 [s] M'mawa mwace khamu lali-
kuru la anthu amene adadza ku-
phwando, pakumva kuti Yesu ali-
nkudza ku Yerusalemu, 13 anatenga
makwata a kanjedza, naturuka ku-
kakomana ndi Iye, napfuula, [t] Hosana;
wolemekezeka Iye wakudza m'dzina
la Ambuye, ndiye Mfumu ya Israyeli.

14 Koma Yesu, [a] m'mene adapeza
kaburu anakhala pamenepo; monga
mulembedwa: 15 [c] Usaope, mwana
wamkazi wa Ziyoni; taona Mfumu
yako idza wokhala pa mwana wa
buru. 16 [d] Izi sanazidziwa akuphu-
nzira ace poyamba; koma pamene
Yesu analemekezedwa, pamenepo ana-
kumbukila kuti izi zinalembedwa za
Iye, ndi kuti adamcitira Iye izi.
17 Pamenepo khamulo limene linali
pamodzi ndi Iye, m'mene anaitana
Lazaro kuturuka kumanda, namuu-
kitsa kwa akufa, anacita umboni.
18 Cifukwa ca icinso khamulo lina-
dza kudzakomana ndi Iye, cifukwa
anamva kuti Iye adacita cizindikilo
ici. 19 Cifukwa cace Afarisi anane-
na wina ndi mnzace, [h] Muona kuti
simupindula kanthu konse; onani
dziko litsata pambuyo pace pa Iye.

*Ahelene afuna kuona Yesu; Iye ayankhapo.*

20 Koma panali [i] Ahelene ena
mwa iwo akukwera kunka kukala-
mbira paphwando. 21 Ndipo iwo
anadza kwa [k] Filipo wa ku Betsaida
wa m'Galileya, namfunsa iye, ndi kuti,
Mbuye, tifuna kuona Yesu. 22 Filipo
anadza nanena kwa Andreya; nadza
Andreya ndi Filipo, nanena ndi Yesu.
23 Koma Yesu anayankha iwo, nati,
[m] Yafika nthawi, kuti Mwana wa mu-
nthu alemekezedwe. 24 Indetu, inde-
tu, ndinena ndi inu, [n] Ngati mbeu ya
tirigu siigwa m'nthaka, nifa, ikhala
pa yokha iyo; koma ngati ifa, ibala
cipatso cambiri. 25 [p] Iye wokonda
moyo wace adzautaya; ndipo wo-
dana ndi moyo wace m'dziko lino la-
pansi adzausungira ku moyo wosatha.
26 Ngati wina anditumikira Ine,
anditsate; ndipo [t] kumene kuli Ine,
komwekonso kudzakhala mtumiki
wanga. Ngati wina anditumikira Ine,
Atate adzamcitira ulemu iyeyu.
27 [v] Moyo wanga wabvutika tsopano;
ndipo ndidzanena ciani? Atate, ndi-
pulumutseni Ine ku nthawi iyi. Ko-
ma cifukwa ca ici ndinadzera nthawi
iyi. 28 Atate, lemekezani dzina lanu.
[z] Pomwepo adadza mau ocokera Ku-
mwamba, Ndalilemekeza, ndipo ndi-
dzalilemekezanso. 29 Cifukwa cace
khamu la anthu akuimirirako, ndi
kuwamva ananena kuti kwagunda.
Ena ananena, Mngelo walankhula ndi
Iye. 30 Yesu anayankha nati, [a] Mau
awa sanafika cifukwa ca Ine, koma ca
inu. 31 Tsopano pali kuweruza kwa
dziko ili lapansi; mkulu wa dziko ili
lapansi adzatayidwa kunja tsopano.
32 Ndipo Ine, [b] m'mene ndikakwe-
zedwa kudziko, ndidzakoka anthu
onse kwa Ine ndekha. 33 Koma
ananena ici ndi kuzindikiritsa imfa
yanji akuti adzafa nayo. 34 Pame-
nepo khamulo linayankha Iye, [e] Tida-
mva ife m'cilamulo kuti Kristu akhala
ku nthawi yonse; ndipo Inu munena
bwanji, kuti Mwana wa munthu
ayenera kukwezedwa? Mwana wa
munthu amene ndani? 35 Pamenepo
Yesu anati kwa iwo, Katsala kanthawi
kakang'ono ndipo kuunika kuli mwa
inu. [f] Yendani pokhala muli nako
kuunika, kuti mdima sungakupezeni;
ndipo woyenda mumdima sadziwa
kumene amukako. 36 [g] Pokhala muli
nako kuunika, khulupirirani kuunika-
ko, kuti mukakhale ana a kuunikako.
Izi Yesu analankhula, nacoka na-
wabisalira. 37 Koma angakhale
adacita zizindikilo zambiri zotere
pamaso pao iwo sanakhulupirira
Iye; 38 kuti mau a Yesaya mneneri
akakwaniridwe, amene anati,

[j] Ambuye, wakhulupirira ndani
kulalikira kwathu?
Ndipo mkono wa Ambuye wa-
bvumbulutsidwa kwa yani?

39 Cifukwa ca ici sanathe kukhu-
lupira, pakuti Yesaya anatinso,

40 [l] Wadetsa maso ao, naumitsa
mtima wao;
Kuti angaone ndi maso, angazi-
ndikire ndi mtima,
Nangatembenuke,
Ndipo ndingawaciritse.

41 [o] Izi anati Yesaya, cifukwa anaona
ulemerero wace; nalankhula za Iye.
42 Kungakhale kotero, ambiri a mwa
akuru anakhulupirira Iye; koma
[r] cifukwa ca Afarisi sanabvomere-
za, kuti angaletsedwe m'sunagoge,
43 [s] pakuti anakonda ulemerero wa
anthu koposa ulemerero wa Mulungu.
44 Koma Yesu anapfuula nati, [u] Iye
wokhulupirira Ine, sakhulupirira Ine,
koma Iye wonditurna Ine. 45 Ndipo
[w] wondiona Ine aona amene anandi-
tuma Ine. 46 [y] Ndadza Ine kuunika
ku dziko lapansi, kuti yense wokhulu-
pirira Ine asakhale mumdima.
47 Ndipo ngati wina akumva mau
anga, ndi kusawasunga, Ine sindi-
mweruza; pakuti [a] sindinadza ku-
dzaweruza dziko lapansi, koma kuti
ndipulumutse dziko lapansi. 48 [b] Iye
amene akaniza Ine, ndi kusalandira
mau anga, ali naye womweruza iye;
[d] mau amene ndalankhula, iwowa
adzamweruza tsiku lomariza. 49 [e] Pa-
kuti sindinalankhula mwa Ine ndekha;
koma Atate wondituma Ine, yemweyu
anandipatsa Ine lamulo, limene ndi-

[a] Mat. 21. 7
[b] Yoh. 3. 14
[c] Zek. 9. 9
[d] Luka 18. 34
Yoh. 2. 22
„ 14. 26
[e] Sal. 89. 35-37
Ezek. 37. 24, 25
[f] Yer. 13. 16
Yoh. 11. 10
Aefeso 5. 8
[g] Yer. 13. 16
Yoh. 11. 10
Aefeso 5. 8
[h] Yoh. 11. 47, 48
[i] 1 Maf. 8. 41-43
Mac. 17. 4
[j] Yes. 53. 1
Aroma 10. 16
[k] Yoh. 1. 44
[l] Yes. 6. 9, 10
[m] Yoh. 17. 1
[n] 1 Akor. 15. 36
[o] Yes. 6. 1
[p] Mat. 10. 39
[r] Yoh. 7. 13
„ 9. 22
[s] Yoh. 5. 44
[t] Yoh. 17. 24
[u] Mat. 10. 40
[v] Mat. 26. 38, 39
[w] Yoh. 10. 30
[y] Yoh. 1. 9
[z] Mat. 3. 17
[a] Yoh. 3. 17
[b] Yoh. 3. 18
[c] Yoh. 11. 42
[d] Deut. 18. 18, 19
[e] Deut. 18. 18, 19





kanene, ndi limene ndikalankhule.
50 Ndipo ndidziwa kuti lamulo lace
liri moyo wosatha; cifukwa cace
zimene ndilankhula, monga momwe
Atate wanena ndi Ine, momwemo
ndilankhula.

## 13 *Yesu asambitsa mapazi a anyamata ace.*

Koma pasanafike phwando la Pa-
skha, Yesu, podziwa kuti [d] nthawi
yace idadza yakucoka kuturuka
m'dziko lino lapansi, kunka kwa
Atate, m'mene anakonda ace a Iye
yekha a m'dziko lapansi, anawa-
konda kufikira cimariziro. 2 Ndipo
pokhala pamgonero, [f] mdierekezi
adatha kuika mu mtima wace wa
Yudase mwana wa Simoni Isikariote,
kuti akampereke Iye, 3 Yesu, podziwa
[g] kuti Atate adampatsa Iye zonse
m'manja mwace, ndi [h] kuti anaco-
kera kwa Mulungu, namuka kwa
Mulungu, 4 [i] anyamuka pamgonero,
nabvula malaya ace; ndipo m'mene
adatenga copukutira, anadzimanga
m'cuuno. 5 Pomwepo anathira
madzi m'nsambidwe, nayamba ku-
sambitsa mapazi a akuphunzira
ace, ndi kuwapukuta ndi copukutira,
cimene anadzimanga naco. 6 Ana-
dza pomwepo kwa Simoni Petro.
Iyeyu ananena ndi Iye, Ambuye,
[l] kodi Inu mundisambitsa ine mapazi?
7 Yesu anayankha nati kwa iye,
Cimene ndicita Ine, sucidziwa tso-
pano; koma [m] udzadziwa m'tsogolo
mwace. 8 Petro ananena ndi Iye,
Simudzasambitsa mapazi anga ku
nthawi yonse. Yesu anamyankha
iye, [n] Ngati sindikusambitsa iwe ulibe
colandira pamodzi ndi Ine. 9 Simoni
Petro ananena ndi Iye, Ambuye, si
mapazi anga okha, komanso manja
ndi mutu. 10 Yesu ananena naye,
Amene anatha kusamba alibe kusowa
koma kusamba mapazi, koma ayera
monse: ndipo [p] inu ndinu oyera, koma
si nonse ai. 11 Pakuti [s] anadziwa
amene adzampereka Iye; cifukwa ca
ici anati, Simuli oyera nonse.
12 Pamenepo, atatha Iye kusambitsa
mapazi ao, ndi kutenga malaya ace,
anaseamanso, nati kwa iwo, Nanga
cimene ndakucitirani inu, mucizi-
ndikira kodi? 13 Inu [t] mundicha
Ine Mphunzitsi, ndi Ambuye: ndipo
munena bwino; pakuti ndine amene.
14 Cifukwa cace, ngati Ine Ambuye
ndi Mphunzitsi, ndasambitsa mapazi
anu, [w] inunso muyenera kusambitsana
mapazi wina ndi mnzace. 15 Pakuti
ndakupatsani inu citsanzo, kuti, monga
Ine ndakucitirani inu, inunso mucite.
16 Indetu, indetu, ndinena ndi inu
[a] Kapolo sali wamkulu ndi mbuye
wace; kapena mtumwi sali wamkuru
ndi womtuma iye. 17 [b] Ngati mudziwa
izi, odala inu ngati muzicita. 18 Si-
ndinena za inu nonse; ndidziwa
amene ndawasankha: koma kuti
colemba cikwaniridwe, [c] Iye wakudya
mkate wanga anatsalimira pa Ine
cidendene cace. 19 Kuyambira tso-
pano ndinena kwa inu, cisadacitike,
kuti pamene citacitika, mukakhulu-
pire kuti ndine amene. 20 Indetu,
indetu, ndinena ndi inu, [e] Iye wola-
ndira amene ali yense ndimtuma,
andilandira Ine; koma wolandira Ine
alandira wondituma Ine.

*Yesu aneneratu kuti Yudase adzampereka.*

(Mat. 26. 20-25. Marko 14. 17-21.)

21 Yesu m'mene adanena izi, ana-
bvutika mumzimu, nacita umboni,
nati, Indetu, indetu, ndinena ndi inu,
kuti [j] mmodzi wa inu adzandipereka
Ine. 22 Akuphunzira analikupenyana
wina kwa mnzace, ndi kusinkha-
sinkha kuti ananena za yani. 23 Ko-
ma [k] mmodzi wa akuphunzira ace
amene Yesu anamkonda analikutsa-
mira pa cifuwa ca Yesu. 24 Pame-
nepo Simoni Petro anamkodola nanena
naye, Utiuze ndiye yani amene anena
za iye. 25 Iyeyu potsamira pomwepo,
pa cifuwa ca Yesu, anena ndi Iye,
Ambuye, ndiye yani? 26 Ndipo Yesu
anayankha, Ndi iyeyu, amene Ine ndi-
dzamsunsira nthongo ndi kumpatsa.
Pamenepo, m'mene anasunsa nthongo
anaitenga naipatsa Yudase mwana wa
Simoni Isikariote. 27 Ndipo pambuyo
pace pa nthongoyo, [o] Satana analowa
mwa iyeyu. Pamenepo Yesu ananena
naye, Cimene uchita, cita msanga.
28 Koma palibe mmodzi wa iwo aku-
seamako anadziwa cimene anafuna,
poti atere naye. 29 Pakuti [r] popeza
Yudase anali nalo thumba, ena anali-
kuyesa kuti Yesu ananena kwa iye,
Gula zimene zitisowa paphwando
kapena, kuti apatse kanthu kwa au-
mphawi. 30 Pamenepo iyeyo m'mene
adalandira nthongo, anaturuka po-
mwepo. Koma kunali usiku.
31 Tsono m'mene adaturuka, Yesu
ananena, [u] Tsopano walemekezeka
Mwana wa munthu, ndipo Mulungu
walemekezedwa mwa Iye; 32 ndipo
[v] Mulungu adzamlemekeza Iye mwa
Iye yekha, adzamlemekeza Iye tsopa-
no apa. 33 Tiana, katsala kanthawi
ndikhala ndi inu. Mudzandifuna-

[a] Mat. 10. 24
[b] Yak. 1. 22, 25
[c] Sal. 41. 9
[d] Yoh. 12. 23
[e] Mat. 10. 40
[f] Luka 22. 3
[g] Mat. 11. 27
[h] Yoh. 8. 42
[i] Luka 22. 27
[j] Mat. 26. 21
[k] Yoh. 19. 26
[l] Mat. 3. 14
[m] v. 12-14
[n] Aefeso 5. 26
[o] Luka 22. 3
[p] Yoh. 15. 3
[r] Yoh. 12. 6
[s] Yoh. 6. 64
[t] Mat. 23. 8, 10
[u] Yoh. 12. 23
„ 14. 13
[v] Yoh. 17. 1, 4-6
[w] Aroma 12. 10
Agal. 6. 1, 2